

CHISINDIKIZO CHACHITATU



Usiku wabwino, abwenzi. Tiyeni tiyimirire tsopano mphindi yokha kwa pemphero. Tiweramitse mitu yathu.

² Atate athu Akumwamba, pamene ife tikuyimva iyo—nyimbo yokongola iyo, ife—ife tikuganiza, Ambuye, za...kuti Inu muli pafupi. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mutilandire ife usikuuno, Ambuye, monga ana Anu, kutikhululukira machimo athu onse ndi zolakwitsa zathu, ndi kutipatsa ife a madalitso Anu, monga ife tiri anthu osowa.

³ Ndipo mu ora lopambana ili limene ife tsopano tikukhalamo, ndipo ife tikuwona, chaka ndi chaka, kukudera derabe, ku dziko lapansi. Ndipo Kubwera kwa Ambuye kukuwalira walirabe, pamene Iye akudziwulula Yekha mu...mu Mawu Ake ndi mu mawonetseredwe Ake. Ife tabweranso kachiwiri, usikuuno, Ambuye, kudzayesera, za msonkhano uno, ndi kudzakupemphani Inu kuti mutsegule kwa ife, Ambuye, Chisindikizo Chachitatu ichi cha Bukhu ili, kuti icho chikakhoze kudziwika kwa ife, kuti ife tikhoze kudziwa choti tichite ndi momwe tingamakhalire moyo, ndi momwe tingakhalire Akhristu abwinoko.

⁴ Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mumupangitse aliyense amene siali Mkhristu muno, usikuuno, kuzindikira chosowa chawo cha Inu. Perekani izi. Ndipo ine—ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Mkhristu aliyense wobadwa kachiwiri azindikire kuti iye ayenera kukhala moyo moyandikira kwambiri kuposa momwe iye wakhalira mmbuyomu, kuti ife tonse tikhoze kukhala mu umodzi uwo wa chikondi Chachikhristu ndi chikhulupiriro.

⁵ Mupereke kuti munthu wodwala aliyense pakati pathu achiritsidwe usikuuno, Ambuye. Iwo akuzindikira chosowa chawo cha Inu. Ndipo ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mudalitse chirichonse chimene chachitidwa kapena kuyankhulidwa, kwa ulemu Wanu ndi ulemelero, mu Dzina la Yesu ife tikupempha izi. Amen.

⁶ Chabwino, kachiwiri, usikuuno, ife tasonkhana pamodzi kachiwiri kwa ichi, u—usiku wa Lachitatu wa sabatayi. Ndipo ife tikudalira pa Ambuye, usikuuno, kwa—kutsanulira kwakukulu kwa madalitso Ake pa Mawu Ake. Ndipo lero ine ndakhala ndikuwerenga, monga mwa nthawizonse, ndi kuyesetsa kuganizira za zinthu zomwe zingakhale zofunikira kwambiri kuziyankhula, ndipo chinthucho, momwe ndingachiyankhulire icho, ndipo kenako kumadalira pa Ambuye kuti apereke kwa ine kutathauzira ndi matanthauzo a—a Mawu awa amene analembedwa. Ndipo ndine wothokoza kwa Iye pa zomwe Iye

watichitira ife kudutsa mu sabatayi, imene ife . . . ya kutsegula kwa Zisindikizo izi.

⁷ Ndipo, ine, mwinamwake icho chingakhale chinthu chabwino ngati Lamlungu mmawa, ku . . . Inu mukudziwa, nthawi zambiri . . . Ife sitimatanthauza kuti tikhale osamvetsetsedwa, koma, inu mukudziwa, iwe . . . Izo zimakhala mwanjira imeneyo. Ndipo kotero, mwinamwake, Lamlungu mmawa, ngati onse amene ali nalo funso mmalingaliro mwawo lokhudza izi, angalilembe ilo ndi kudzalipereka ilo pa tebulo apa, Loweruka usiku, ndipo kotero kuti ine ndidzakhoke kudzawona lomwe ilo liri. Ndiyeno ine ndidzayesetsa kukuyankhirani ilo, Lamlungu mmawa, Ambuye akalola. Ine ndikuganiza kuti icho chingadzakhale chabwinoko kuposa chimene ife timakonzekera, chifukwa nthawizina sizimamvetsetsedwa, inu mukudziwa. Ndipo kotero mwanjira imeneyo ine ndidzakhala . . . Izo zingadzakhale zabwinoko kuti ine ndidza—ine ndidzazitenge izo mowongoka, inu mukudziwa. Izo zingadzakhale basi momwe ziyenera kukhalira. Chifukwa, nthawizina, tsopano . . .

⁸ Winawake anayimba lero ndipo ananena, kuti—kuti, anayimba ndipo amafuna kudziwa ngati izo zinali zoona, kuti, “Pamene a—Mkwatulo udzachitike, padzangokhala mmodzi mu Jeffersonville ndi mmodzi mu New York, ndipo ena onsewo kutsidya kwa nyanja.” Kotero, mukuona, izo sizinamvetsetsedwe basi. Kenako winawake ananena, kuti, “Loweruka usiku, ngati Ambuye adzapereke kwa ife Chisindikizo chotsiriza, ndiye Yesu adzakhala pano Lamlungu mmawa.” Mukuona? Kotero ndicho—ndicho . . . Inu mukuona, inu—inu simu . . . Izo, siziri chomwecho. Ndipo inu musati . . . Izo siziri.

⁹ Ife sitikudziwa. Ngati aliyense akuwuzani inu kuti akudziwa tsiku limene Iye akubwera, inu mudziwe kuti iwo akulakwitsa, kuyamba ndi kuyamba, chifukwa palibe aliyense amene akudziwa zimenezo. Koma ife tikufuna kuti tizikhala moyo, lero, ngati kuti zichitika pakali pano.

¹⁰ Ine ndikhala ngati ndakutembenezani mozungulira kwa miniti, kotero konzekerani. Ine—ine ndikukhulupirira Yesu abwera mkati mwa, asanakwane, maminiti atatu kuchokera pakali pano, a nthawi Yake. Inu mukudziwa kutalika kwake momwe kungakhalire? Pafupifupi zaka sarte-faivi. Mwaona, zaka sauzande ndi tsiku limodzi lokha, kwa Iye, mukuona.

¹¹ Kotero, pamene inu mukumumva mtumwi kumbuyo kuno akuti, “Nthawi ili pafupi,” cha apa, “nthawi ili pafupi.” Mtumwiyo ankanena zimenezo mwa Vumbulutso. Inu mukudziwa kuti izo zakhala utali wotani? Iyo siyinati . . . Limenelo linali dzulo chabe, kwa Mulungu, osati masiku awiri nkomwe.

¹² Ndipo, mwaona, ngati ali maminiti atatu, osakwanira maminiti atatu a Kudza Kwake, mwaona, zimenezo zingakhale zaka sarte, pafupifupi, kwa ife, kapena chinachake mwa dongosolo limenelo. Ndipo taonani momwe, maminiti atatu angakhalire kwa Iye: Iye wadzuka kale, kuti azibwera. Kotero ife, inu...nthawizina pamene iwe uwerenga apa, Iye akuyankhula mmanenedwe a Mawu, mwaona, osati mwa manenedwe athu.

¹³ Ndiyenso ngati nditadziwa kuti Iye anali kubwera mawa usiku, mawa usiku, mawa ine ndikanadzawerenga ndi kumupempha Iye kuti andipatse ine Uthenga wa Chisindikizo Chachinai. Ndipo ndikanadzabwera kuno ndi kudzalalikirira Icho, chimodzimodzi basi. Mukuona? Ine—ine ndikufuna ndizichita tsiku lilirilonse chokhacho chimene ndikanamachita ngati Iye akubwera. Ndipo ine sindikudziwa malo ena abwinoko kuposa kudzatengedwa pa malo antchito pomwe, mwaona, pa malo antchito pomwe. Kotero ife tizingopitirirabe kufikira Iye adzabwere.

¹⁴ Nthawizina pamene ife tikungowerenga, ndipo, tsopano, muzikhala osamalitsa kwenikweni. Ndipo pamene inu mukuwerenga, muzitenga matepi, muziwamvetsera iwo mwatcheru kwenikweni. Chifukwa, inu mudzadzimvetse izo pa tepi, chifukwa iwo akhala akuwayimba matepi amenewo mobwereza bwereza, ndipo iwo ndi abwino kwenikweni ndiponso omveka. Kotero, inu mukamvetsera izo momveka bwino pamenepo.

¹⁵ Tsopano, aliyense ali mu chikondi ndi Khristu, ine ndikuyembekeza, usikuuno, ndipo aliyense akumukonda Iye.

¹⁶ Ine ndikuuzani inu chimene, nthawizina, chimene chimawasokoneza anthu, kuti winawake amabweramo amene sanamvetsere gawo loyamba la msonkhano, inu mukuona. Ndiye iwo amabweramo ndipo iwo amakumva iwe ukulozera mmbuyo, kukagunda chinachake, cha mmbuyo, ndipo kenako iwo amatenga chimenecho, chimene chayankhulidwacho, ndipo sanamvetsere gawo loyambalo. Ndiye izo zonse zimakhala zosokoneza kwa iwo, mukuona, pamenepo. Ndipo iwo amaganiza kuti chinachake chinanenedwa mosiyana, koma Icho—koma Icho si choncho.

¹⁷ Kotero ngati muli ndi funso limene inu simukulimvetse, mungolilemba ilo pa chidutswa cha pepala. Mudzaliyike ilo muno, nthawi iliyonse pakati pa lero ndi Loweruka usiku. Ndipo ine ndidzayesetsa, Lamlungu mmawa, kuti... Ngati ziri zododometsa pang'ono, inu mudzati, "Chabwino, ine ndikungodabwa chimene *ichi* chimatanthauza apa. Ine sindinachimvetse icho." Inu mukudziwa chimene ine

ndikutanthauza. Ndiye ine ndidzayesetsa kukuyankhirani inu chimenecho, Lamlungu mmawa, Ambuye akalola.

¹⁸ Tsopano, usikuuno ife tiwerenga kuchokera mu Mawu akale odalitsidwa awa kachiwiri, mu mutu wa 6. Ndipo ife tiyambira usikuuno ndi Chisindikizo Chachitatu. Ndipo imeneyo ndi ndime ya 5, ndime ya 5 ndi ya 6.

¹⁹ Ndipo mawa usiku ife tidzatsekera okwera anayi; kavalo woyera, ndi kavalo wofiira, kavalo wakuda, ndi kavalo wotumbululuka.

²⁰ Ndipo ine ndikufuna kunena ichi. Kuti, nthawi iliyonse, ngakhale kufikira mmawa uno, pafupifupi... Oh, ine ndimadzuka molawirira kwenikweni, kwenikweni ndipo ndimapita kukapemphera zinthu zisanakondowezeke, ndi kumangopitiriza kupemphera kudutsa mu tsiku. Koma mmawa uno, molawirira, Mzimu Woyera unabwera kumene ine ndinali. Ndipo momveka basi monga chirichonse, ine—ine ndinachiwona Chisindikizo china ichi chikutseguka tsopano, ndendende basi. Tsopano—tsopano—tsopano, Iye amandimva ine, ine ndikudziwa. Ndipo ndine woyamikira kwambiri.

²¹ Tsopano, inu mungokumbukira kuti pali chinachake chikuchitika. Kuti, ine—ine ndikuyembekeza kuti inu mukuzigwira izo, mwaona, pamenepo... kuti pali chinachake chomwe chikuchitika. Ine ndikungofuna kuti ndidzawuyese mpingo uno nthawi ina, ndi kudzawona ngati iwo angakhoze kwenikweni kugwira chinachake icho chisanachitike kwenikweni. Tsopano kumbukirani, kumbukirani zomwe ine ndakuuzani inu. Ndipo, tsopano, Ambuye atithandize ife.

²² Tsopano mu ndime ya 5.

Ndipo pamene anatsegula chisindikizo chachitatu, ine ndinamva chamoyo chachitatu chikuti, Bwera... udzawone. Ndipo ine ndinawona, ndipo taonani, kavalo wakuda; ndipo iye amene anakhala pa iye anali nazo zoyezera mdzanja lake.

Ndipo ine ndinamva liwu pakati pa zamoyo zinayi, likuti, muyezo wa tirigu wogudwa ndi ndalama, ndi miyezo itatu ya barley yogudwa ndi ndalama; koma onetsetsa kuti iwe usapweteke mafuta ndi... vinyo.

²³ Tsopano tiyeni tiyike maziko a izi pang'ono pokha, ndi pa Zisindikizo zimene ife tazidutsa. Chifukwa, basi monga ngati mmibadwo ya mpingo, bwanji, ife timayesetsa kuyika maziko, kuti tikhale ngati tikuzilumikizitsa izo, kufikira inu mutakhoza... Umo ndi momwe mibadwoyo ikukhalira makamaka Mu Lemba, umodzi umalowererana ndi umzakewo, basi monga chomwecho. Monga kukwera makwerero, ndi kukwera pa sitepe, kani; umodzi kumatsikira pansu kwa umzake, ndi kumabwerera mmbuyo monga chomwecho, pamene iwe ukupita chokwera sitepe.

²⁴ Ndipo tsopano, Zisindikizo izi, a...Ndizo bu—Bukhu la Chiwombolo, losindikizidwa. Aliyense akumvetsa zimenezo? [Osonkhana akuti, “Amenei.”—Mkonzi]. Ndipo Bukhu ili ndi losindikizidwa ndi Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwi. Ilo ndi Bukhu losindikizidwa kasanu ndi kawiri. Mukuona?

²⁵ Ndipo tsopano kumbukirani, monga ife tinawonetsera izo kwa inu, ndipo tinazitenga izo kuchokera ku Yeremiya ndi onse. Tsopano, iwo, pamene iwo anali...Iwo ankalemba monga *chonchi*, pa chidutswa cha—cha cholembapo, kapena pepala, kani; kapena, osati pepala, koma icho chimakhala chikopa. [M’bale Branham akugwiritsa ntchito mapepala kuwonetsera kukulunga ndi kusindikiza kwa mpukutu—Mkonzi]. Ndipo iwo ankachikulunga icho, monga *chonchi*. Tsopano icho...Ndiyeno pa mapeto pake pankasiyidwa monga *choncho*; zimenezo zinkasonyeza chimene chiri mmenemo. Ndiye chotsatiracho chinkatenga mtundu womwewo wa malo, kukulungidwa mwanjira yomweyo, chinkakulungidwa monga *chomwecho*. Ndipo kenako, pamapeto apa, icho chinkang’ambidwa monga *choncho*, ndi kusiya chimodzi china.

²⁶ Chabwino, limenelo linali Bukhu losindikizidwa kasanu ndi kawiri. Tsopano ife tinalibe Mabuku monga *awa* kufikira posachedwapa. Mabuku mu nthawi yakale anali mipukutu. Iwo anakukulungidwa. Ndiyeno pamene iwo akufuna phunziro kapena chirichonse...Monga ngati—ngati Baibulo lakulungidwa, iwe ukufuna kuwerenga Bukhu la Yesaya; iwe unkatembenezira pansu apa ku Yesaya, kenako nkulifutukula Ilo monga *choncho*, ndi kuwerenga Ilo. Ndipo ili ndi Bukhu la Chiwombolo losindikizidwa kasanu ndi kawiri.

²⁷ Ndipo tsopano ife tikupeza kuti Mwanawankhosa akutulukira, akudzatenga Bukhulo kuchokera mdzanja la Iye amene anakhala pa Mpandowachifumu, ndipo akudzamatula Zisindikizo, ndi—ndi kumasula...ndi kumasula Izo, kumasula Zisindikizozo kwa anthu.

²⁸ Ndipo Zamoyo zinayi zimenezo zitakhala pamenepo, zomwe ife tinazitenga mmibadwo ya mpingo, Zamoyo zinayi zomwezo, inu mukuziwona izo njira yonse kudutsa mu Lemba, ndipo Izo ndi Zomwe zikumachita kulengeza kwa Zisindikizo izi pamene zikumatulidwa. Tsopano, ndipo ife tikuliwona ilo kuti ndi a—Bukhu la Chiwombolo.

²⁹ Ndiye ife tinabwerera mmbuyo ndi kukatenga a—Muwomboli Wachibale, ndipo tinamutenga Iye, kuti tiwone yomwe inali ntchito Yake. Ndipo tsopano kwa zaka zonsezi, Khristu wakhala akuchita ntchito ya Muwomboli Wachibale. Tsopano, nonse amene mukumvetsa zimenezo, nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Iye wakhala akuchita ntchito ya Muwomboli Wachibale.

³⁰ Koma idzafika nthawi pamene ntchito yowombola idzakhala itatha. Ndipo pamene ntchito yowombola idzatha, ndiye Iye adzasiya Mpandowachifumu wa Mulungu, pamene Iye wakhala tsopano. Koma umenewo si Mpandowachifumu Wake. “Iye amene agonjetsa adzakhala nane Ine mu Mpandowachifumu Wanga, monga Ine ndagonjetsa ndipo ndakhala pa Mpandowachifumu wa Atate Anga.” Umenewo si Mpandowachifumu Wake. Umenewo ndi wa Mzimu, Mulungu. Khristu, Mwanawankhosa, iwo si wa Iye. Iye ndi Mulungu m’tuphi, mwaona; amene ali Mulungu yemweyo, atapangidwa thupi. Tsopano, Iye akudzuka kuchokera pa mpando. . .

³¹ Choyamba, kulengezako kunapita pamenepo, pakuti, “Ndani angakhoze kubwera ndi ku- . . . ndi kudzatenga Bukhu ili la Chiwombolo?” Mwaona, kwa dongosolo lonse la chiwombolo, kuchokera kwa Adamu, zonse zimene Adamu anataya.

³² Kunalibe kanthu kotayika kufikira Adamu atabwera. Ndipo pambuyo pa Adamu, zonse zinatayika, pa dziko lapansi. Ndipo chirichonse pa chirengedwe cha dziko lapansi chinatayika. Ndipo chirichonse chinagwa limodzi ndi Adamu, chinawoloka phompho, mwakuti palibe chimodzi chikanakhoza kubwerera, panalibe njira nkomwe. Munthu, pamene iye anachimwa, iye anasiya njira yake, iye sanasiye njira yobwererera ya iyemwini. Ndiyeno pamenepo. . .

³³ Pamene funso ili linafunsidwa; Yohane mvumbulutsi, amene . . . mneneri Yohane, anali mmasomphenya ndipo anawona zimenezo. Ndipo kunalibe munthu Kumwamba, panalibe munthu pa dziko lapansi, panalibe munthu pansa pa dziko lapansi, kapena aliyense, amene anali woyenera ngakhale kuyang’ana pa Bukhulo. Mukuona? Tsopano tangoganizani za zimenezo! Kenako Mwanawankhosa akubwera patsogolo, ndipo Iye akudzatenga Bukhulo. Tsopano Yohane anapemphedwa kuti asalirenso. Iye anati, “Taona, Mkango wa Yuda walakika, ndipo—ndipo Iye akhoza kulitenga Bukhulo ndi kulitsegula Ilo.” Chotero, iye anatembenuka kuti ayang’ane pa Mkango, ndipo anawona Mwanawankhosa. Mkuluyo anayitana, anati, “Mkango walakika.” Koma pamene iye anabwera ndi kudzayang’ana, uyo anali Mwanawankhosa akutulukira kuchokera ku Mpandowachifumu.

³⁴ Tsopano, iye anali asanachizindikire konse Icho poyamba. Chifukwa chiyani? Iye anali ali kumbuyo uko, mu kuchita Kwake kwa ntchito Yake ya umkhalapakati; pakuti Iye anali akuwukha magazi chifukwa cha anthu, akuwapembedzera anthu, kufikira moyo wotsirizawo, umene unayikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, utadzabwera mkati. Kudzangokhala ambiri a iwo kumeneko, ndipo ndi zimenezo. Ndizo zonse. Enawo sadzafuna nkomwe kuti abwere mmenemo; iwo alibe chikhumbo choti abwere

mnenemo. Ndipo kotero, ndiye, pamene moyo wotsiriza uwo udzabwera mnenemo, ndiye kuti nthawi ya chiwombolo yatha.

³⁵ Zikadzatero Mwanawankhosa adzatulukira kuti adzatenge maufulu Ake kwa zomwe Iye waziwombola, ndipo ndicho chirengedwe chonse. Dziko lapansi ndi chirichonse ndi za Iye. Mukuona? Iye waliwombola ilo ndi Magazi Ake Omwe. Ndipo pamene Iye anabwera pamenepo kuti adzalitengea Bukhu ili, kuti adzalitsegule Ilo, bwanji, mai, iwo anali... Yohane sanalirensa. Ndipo iye anayang'ana, ndipo Mwanawankhosa uyu anali Mwanawankhosa wophedwa. Iye anali ataphedwa kale, koma iye anali wamoyo aponso. Ndipo tsopano ife tinapeza kuti mwanawankhosa wophedwa ndi mwanawankhosa wamagazi, akuwukha magazi paliponse. Iye anali ataphedwa. Atatha Iye kuphedwa, Iye anali atawuka kachiwiri. Iye anali atakhala pa Mpandowachifumu, titi, mmbuyomo kuseri kwa Mpandowachifumu, monga *chonchi*, akupembedzera miyoyo yonse iyo imene ikanati idzabwere. Ndiye pamene mmodzi wotsirizayo anali apa, ndipo iyo inali itatsirizidwa, a... Mulungu anagwirabe Bukhu la Chiwombolo. Mukuona? Tsopano Iye akungochita ntchito ya Wachibale tsopano.

³⁶ Monga, Boazi anapita kumusi, ndipo Rute anali atangokhala pamenepo akuyembekezera kufikira Boazi... ine ndikutanthauza, Boazi anachita... wachibale, ntchito yowombola. Mukukumbukira ine ndikulalikira zimenezo, osati kale kwambiri? Rute, akukunkha; ndipo, Rute, chirichonse chimene iye ankachita; ndipo mpaka mmusi, ndipo chinthu chotsiriza chinali, Rute, kudikirira. Mukukumbukira momwe ine ndinazifanizitsira izo mu Mpingo? Pamene, Boazi ankapita kukagwira ntchito ya muwomboli wachibale. Iye anachita zimenezo; anavula nsapato yake ndipo anachitira umboni, ndipo anamuwombola Naomi, ndipo, pochita zimenezo, anamutenga— anamutenga Rute. Tsopano, kotero, Rute ankangodikirira, chifukwa iye anali atagwira kale ntchito. Iye anali atachita zinthu zina zonse izi, koma apa iye anali akudikirira tsopano. Ndiyeno pamene... Mpingo ukuyembekezera, ukupuma (ambiri a iwo, ochuluka a iwo, mu fumbi la dziko lapansi), pamene Iye akuchita ntchito Yake ya Muwomboli Wachibale.

³⁷ Tsopano dziko likupitabe moyipa kwambiri. Ndipo tchimo likuwunjikana, ndi—ndi matenda, ndi mavuto, ndi imfa, ndi chisoni. Amuna opanda Umulungu ndi akazi opanda Umulungu akufa mmusi momwe. Khansa ikuwadya iwo, ndi china chirichonse, pamene iwo sakukhoza kusunga chikhulupiriro chokwanira kuti afikire kumeneko ndi kukazigwira izo.

³⁸ Tsopano zindikirani. Koma kenako zitatha izo zonse, itatha ntchito Yake ya umkhala paka... Kupembedzera kwake kutachitika, Iye akutulukira, akudzatenga Bukhulo kuchokera mdzanja la Iye. Ndiyeno Yohane, ndi chirichonse Kumwamba, ndipo zinayamba... Miyoyo ya pansu pa guwa inayamba

kufuula. Ife tidzazipeza zimenezo mu Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, aponso. Ndi momwe iwo ankasangalalira! Ndipo—ndipo iwo anagwa pansi, akuluwo, ndipo anatsanulira mapemphero a oyera. Ndipo miyoyo ya pansi pa guwa inafuula, “Woyenera muli Inu, chifukwa Inu mwatiwombolera ife kwa Mulungu! Ndipo ife tikubwerera ku dziko lapansi, kukakhala monga mafumu ndi ansembe.” Oh, apo panali chachikulu. . .

³⁹ Ndipo Yohane anati, “Aliyense Kumwamba, chirichonse pansi pa dziko lapansi, ndi chirichonse,” chinamumva iye akulemekeza Mulungu za icho. Yohane ayenera kuti analipeza dzina lake Pamenepo, inu mukudziwa. Nthawi yonseyo!

⁴⁰ Ndiye iye anati, “Iye ndi woyenera kutenga Bukhu la Chiwombolo.” Tsopano ilo si la Woweruza aponso. Ilo ndi la Muwomboli, ndipo Iye wachita kale ntchito ya chiwombolo.

⁴¹ Tsopano Iye akupita kukawuwonetisa Mpingo chimene Iye wachita. Amen. Mukuona? Ndiye Iye akungotenga. . . Koma Bukhulo ndi lotsekedwa. Palibe aliyense ankadziwa, nkomwe. Iwo ankadziwa kuti Ilo linali Bukhu la Chiwombolo, pa Ilo pamenepo, koma Ilo ndi lakuti lidzawululidwe mmasiku otsiriza. Molingana ndi Chivumbulutso 10, mngelo wachisanu ndi chiwiri adzapatsidwa Uthenga wa Ilo. Chifukwa, Ilo linanena, kuti, “Mu nthawi ya kuwomba kwa m’badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri, mngelo wachisanu ndi chiwiri, pamene iye adzawomba, zinsinsi zonse za Mulungu ziyenera kudzatsirizidwa, pakuwomba kwakeko.” Ndiye, pamene Ilo lawululidwa, Mngeloyo anadzatsika pansi kuchokera Kumwamba, amene anali Khristu. Tsopano kumbukirani, mngelo uyu ali pa dziko lapansi, wamthenga.

⁴² Pansi akubwera Khristu, inu mukumuwona Iye mu mutu wa 10 wa Chivumbulutso; akudzayika phazi limodzi pa mtunda, linalo pa nyanja; utawaleza pa mutu Pake, maso ngati. . . ndi mapazi ngati moto, ndi zina zotero; akukweza mmwamba dzanja Lake, ndipo akulumbira pa Iye amene ali ndi moyo kwanthawi zanthawi, ali pa Mpandowachifumu, kuti, “Nthawi siyidzakhalaponso.” Ndipo pamene Iye akutenga lumbiro ili, Mabingu Asanu Ndi Awiri akuyankhula maliwu awo.

⁴³ Ndipo wolembayo, amene, pamene Yohane anatengedwera mmwamba, ankayenera kulemba zomwe iye ankaziwona. Iye anayamba kuti azilemba. Iye anati, “Usalembe Zimenezo.” Chifukwa. . . “Usalembe Zimenezo.” Izo ndi zo-. . . Iye anati, “Usindikize Zimenezo.” Mu chiyani? “Usindikize. Usanene Zimenezo.” Mukuona, Izo ndi zoti zidzawululidwe, koma Izo sizinalembedwe nkomwe mu Mawu.

⁴⁴ Ndiyeno pamene Iye anayamba kutsegula Zisindikizo, ife tikupeza kuti, izo zonse zinali zododometsa. Mukuona? Pamene Iye anatsegula Chisindikizo Choyamba, iye anaganiza, “Tsopano apa Ichu chinena, ‘Ndipo padzachitika icho *chakuti-ndi-chakuti*

chidzatenga mpandowachifumu, ndipo *china* chidzachita *ichi*, ndipo *ichi* chidzachita *icho*.”

⁴⁵ Koma pamene icho chinali, apa iye anapita, kavalo woyera, akukwera, ndipo wokwera ali pa iye. Chabwino, “Iye anali nawo uta mdzanja lake; ndipo iye anapatsidwa korona, patapita kanthawi,” iye anati. Ndizo zonse.

⁴⁶ Ndipo Mwanawankhosayo anatembenukira mmbuyo kachiwiri, ndipo anasolola Chisindikizo china, ndipo apa panatulukira wakuda... wokwera pakavalo wofiira. “Ndipo iye anali nalo... anapatsidwa a—lupanga; ndipo iye anali kupita kukachita nkondo; ndipo anapatsidwa mphamvu yaikulu, ndi kuchotsa mtendere pa dziko lapansi, ndi kumaphana wina ndi mzake.” Icho chinali ngati... chinthu chachinsinsibe (si choncho izo?), pamene Iye anadzatsegula Icho.

⁴⁷ Ndiyeno akupitirabe, ndipo anati, “Mu tsiku basi asanachitike Mabingu Asanu Ndi Awiri awa, zinsinsi zonse apa zidzawululidwa.”

⁴⁸ Tsopano taonani. Ndiye ife tikupeza, monga ife takhala tikuwerengera, kuti, kutsika kudutsa mmibadwo, ife takhala nawo okonzanso, osati aneneri. Okonzanso! Ndipo udindo uliwonse umatenga yake yake—ntchito yake yake.

⁴⁹ Monga ngati munthu amene ali—woyankha mafoni, iye kwenikweni si wokonza magetsi. Iye akhoza kuchita kantchito pang’ono pa zimenezo. Ndipo monga, ngati munthu ali woyika nthambo, chabwino, iye ndithudi... Munthu amene ali wokumba maenje a mapolo, ndipo sanachitepo nkomwe ntchito iliyonse ya nthambo, zingakhale bwino atatalikirana nayo nthambo; koma iye akhoza kuchita ntchito pang’ono yosamalira kapena chinachake.

⁵⁰ Koma pamene Chinthu chenichenicho chiri choti chidzawululidwe pa tsiku lotsiriza, la gawo lotsiriza la Mpingo, ndi pamene Mulungu wanena kuti Iye akanadzatumiza kwa ife, malingana ndi Malemba. Ndipo tazifufuza izo modutsa ndi modutsa, kuti Iye ananeneratu kuti Mzimu wa Eliya ukanadzabwerera mwa munthu winawake. Tsopano, ine ndikuganiza kuti izo zapangidwa momveka bwino basi. Ndipo ife... Ndipo tikuyembekezera zimenezo kuti zichitika; kwinakwake, munthu wodzozedwa, mmasiku otsiriza, kuti adzawuka. Tsopano inu mudzamva zambiri za otentheka ndi zina zirizonse, koma izo basi—zimangoyesera basi ku... Ndi mdierikezi, akuyesetsa kuti akuchotseni kwa weniweniyo akadzati wafika kuno, mwaona. Koma iye adzazindikiritsidwa bwino bwino. Inu mukudziwa chimene Eliya anali; ndipo penyani zimenezo, ndipo inu—inu mudzadziwa. Ndiyeno pamene iye... Tsopano, Osankhidwa adzadziwa.

⁵¹ Osati enawo; iwo ndithudi sadzachita zimenezo. Iwo adzachiphonya Icho, mailosi milioni. Monga... Ife takhala

tikudutsamo monsemo, ndipo tinawonetsa momwe iwo anamuphonyera Yohane, momwe anamuphonyera Eliya, momwe iwo anamuphonyera Yesu, momwe iwo anawaphonyera iwo njira yonse motsatira. Ndipo iwo adzachita chinthu chomwecho, chifukwa Baibulo linati iwo akanadzatero. Mukuona? Koteri ndiye, mu nthawi imeneyo, Izo zidzakhala zodzichepetsa kwambiri. Izo zidzakhala zophweka kwambiri. Izo zidza... chimene chidzawapangitse anthu kugwa kuchoka kwa Icho. Ndi zophweka kwambiri kwa iwo. Ife tikupeza kuti, ndipo nthawizonse, pamene anthu akhala anzeru ndi ophunzira, ndi kudziwa zambiri, ndiye iwo basi... Ndiwo basi mtundu umene umaziphonya izo, inu mukudziwa. Mukuona?

⁵² Yesu sanawatengepo konse anthu a mtundu umenewo (kukhala) ophunzira Ake. Iye ankatenga anthu osaphunzira, asodzi, ndipo palibe amene anali wolumikizana ndi mipingo yawo ndi zinthu. Iye ankangotenga anthu wamba, otolera misonkho, ndi alimi, ndi asodzi, ndi ena otero, kuti agwire ntchito Yake. Mukuona? Chifukwa, iwo—iwo amadziwa kuti siali kanthu, ndiye Iye akhoza kupanga chinachake kuchokera mwa iwo, mwaona. Bola ngati iwo azipitirira kumazindikira kuti iwo siali kanthu, ndiye Mulungu akhoza kugwira ntchitoyo.

⁵³ Koma pamene iwo afika poganiza kuti iwo akudziwa chinachake, ndiye, “Iwe sukudziwa kanthu kamene iwe umayenera kukadziwa,” Baibulo limatero. Ndipo koteri, ndiye, ife—ife tikupeza zimenezo.

⁵⁴ Ndipo tsopano, ife tikupeza, ndiye, kuti zinsinsi izi zikuyenera kuti ziwululidwe.

⁵⁵ Ndipo ndi chifukwa chiyani amuna ena awa, Wesley, Luther, ndi okonzanso opambana amenewo, amene anabweretsa kulungamitsidwa, kuyeretsewa, m'badwo wa Chipentekoste ndi ubatizo wa Mzimu Woyera ndi zinthu, ndi chifukwa chiyani iwo sanazigwire izi—Mauthenga awa? Ndi chifukwa chiyani sanawapeze Iwo? Chifukwa iwo anali okonzanso. Mukuona?

⁵⁶ Basi monga, zitengereni izo ku mbali inayo, uko kunali anthu amene anabwera umo amene anali “anali nayo mphamvu monga mafumu, koma sanali mafumu.” Mukuona? Mukuona? Inu muyenera kuzindikira kalongosoledwe ka Baibulo ka chirichonse. Mukuona? Tsopano penyani. Koma, ichi, chifukwa chimene mbali zonse zosochera, za gawo lachinsinsi zokhudza kulungamitsidwa, gawo lachinsinsi la kuyeretsewa, gawo lachinsinsi la ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo, bwanji, ndi mtundu wanji umene...? Kodi Eva anadya apulo, kapena kodi iye anadya makangaza, kapena chinachake? Mukuona? Kodi...? Kodi mbewu ya serpenti inali chiyani? Ndipo—ndipo kodi ubatizo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” kapena Dzina la “Ambuye Yesu,” wolondola? Ndipo, oh, mazana a zinthu zimenezo, zakhala zitasiyidwa ndi mapeto omasuka. Mukuona?

⁵⁷ Ndiyeno mu ora lotsiriza, munthu uyu ali woti adzabwera ndi kudzachiwulula chinthucho, mukuona, kudzawatenga Malembawo. Izo zidzazindikiritsidwa bwino bwino. Penyani. Inde, bwana. Ndipo, tsopano, icho sichidzakhala chinthu chotchuka, chachikulu tsopano. Zimawoneka ngati, apa mu Baibulo, icho chidzakhala chinachake chachikulu.

⁵⁸ Chinali chachikulu bwanji chimenecho, pamene Yohane ankayenera kubwera kumusi uko ndi kudzabatiza! Tangoganizani tsopano. Aneneri, mmbuyomo, njira yonse mmbuyo, Yesaya, Malaki, ndi onse a iwo ankayankhula za iye, pamene iye akanati adzabwere. Ndipo pamene iye anatero, munthu payekha, wokalamba, wosaphunzira, ali ndi ndevu kunkhope kwake konse, ali ndi tsitsi nyankhalala ngati chiyabwe chosawoneka bwino, ndi chidutswa chachikulu chakale cha chikopa chankhosa chitakulungidwa momuzungulira iye; wopanda maphunziro nkomwe, sanapite konse ku sukulu tsiku limodzi mu moyo wake, monga momwe ife tikudziwira. Mukuona? Apa iye akubwera, akuchokera ku chipululu, wosalandiridwa nkomwe mochuluka pa guwa, ndipo anayima kunja uko pa mtsinje wa Yordano ndipo anayamba kuyitanira anthu kuti akalape. Inu mungalingalire!

⁵⁹ Baibulo linanena, kuti, “Chirichonse chidzakhala chopambana kwambiri mu tsiku limenelo, ngakhale mpaka malo onse okwera adzapangidwa kukhala otsika, ndipo malo onse otsika adzakwezedwa.” Inde bwana. “Ndipo malo onse okumbika adzakhala osalazidwa.”

⁶⁰ Bwanji, ine ndikukhoza kulingalira ndikuwawona iwo kunja uko, akumaganiza kuti Yohane akanadzatulukira, kapena wotsogolera kudza wamkulu uyu wa Khristu, ndi kudzangotenga chipululu chonse ndi kuchisalaza icho, ndi kudzayikamo udzu kachiwiri. Mukuona? Oh, iwo, ine ndikulingalira kuti iwo anali nazo izo zonse zitakonzedwa, pafupifupi monga iwo aliri nazo lero.

⁶¹ Koma, izo zinali zodzichepetsa kwambiri, ngakhale atumwi anaziphonya izo. Iwo anati, “Chabwino, bwanji nanga Lemba limati, ngati a... Inu mukupita kumeneko kukaperekedwa tsopano? Nanga bwanji Lemba limanena kuti—kuti Eliya ayenera kubwera poyamba?”

⁶² Iye anati, “Iye anabwera kale, ndipo inu simunazidziwe zimenezo. Ndipo, Mwana wa munthu, iwo adzamuchitira chinthu chomwecho. Koma, Yohane,” Iye anati, “anachita basi zimene zinayikidwa kwa iye kuti azichite. Ndipo iwo anamuchitira iye basi zomwe iwo ankayenera kuti azichite. Ndipo,” anati, “koteri momwemonso ayenera Mwana wa munthu kuzunzidwa.”

⁶³ Bwanji, uko kunalibe, ine ndikuganiza, gawo limodzi mwa atatu la mtundu wonse wa Ayuda amene anadziwa konse kuti

Yesu Khristu anali pa dziko lapansi. Sanatero...Iwo mwina akhoza kukhala kuti anamva za wotentheka wina cha kumusi uko penapake, koma iwo sanapereke chidwi chirichonse kwa izo, amangopitirirabe. “Iye anabwera kwa Ake Omwe, ndipo Ake Omwe sanamulandire Iye ayi.” Tsopano, apo ndi pamene ine ndikukhulupirira ngakhale...Tsopano, iwo sananene kuti Iye akanadzabwera mwachinsinsi.

⁶⁴ Koma Mkwatulo udzakhala chinsinsi. Kotero ngati icho chinali chinsinsi kwambiri, pamene Iye anabwera, nanga ndi mochuluka bwanji Mkwatulo udzakhale wosadziwika! Mukuona? Iwo sadzadziwa izo. Mwachindunji iwo adzati, “Chabwino, ine ndimaganza ife timayenera kukhala ndi Mkwatulo. Ndipo ziweruzo zonsezi pa dziko lapansi?”

⁶⁵ Iye adzati, “Iwo wachitika kale, ndipo inu simunazidziwe izo.” Mukuona? Izo zidzakhala chomwecho, basi monga ngati wakuba usiku.

⁶⁶ Monga a—bukhu limene ndinawerenga, nthawi ina. Kodi ilo limatchedwa chiyani? *Romeo ndi Juliet*, kodi ndicho chimene ilo linali, kapena chinachake? Iye anayika, anakweza makwerero apo pambali pa nyumba, mwanjira yina. Ine nd-... Linali kalekale. Ndipo anabwera, anadzatenga wake...kuti adzamatulutsire iye panja nthawi ya usiku.

⁶⁷ Tsopano, umo ndi momwe iwo udzati—iwo udzachitikire, ndipo udzakhala utapita. Osati, iwo adzatumiza gulu la Angelo pansi, ali ndi makasu ena, ndi kudzakumba manda. Baibulo linati, “Ife tidzasinthidwa, iwe usanaphethire nkome diso lako.” Mkuthwanima kokha, zonse zidzakhala zitatha, mwamsanga chomwecho.

Mudzangoti, “Winawake wasowa.”

⁶⁸ Chabwino, ine ndikukhoza kuganiza kuti ngati tingakhoze kufufuza dziko lonse, lero, pakhala pali anthu faivi handiredi akusowa pa dziko lapansi tsiku lililonse, mukuona, iwo sakudziwa kanthu kalikonse za izo. Iwo akungopezeka, akusowa.

Chabwino, sipadzakhala ochuluka kwambiri amene ati adzapite mu Mkwatulo umenewo.

⁶⁹ Tsopano, ine sindikufuna kuti ndikuwopsyezeni inu, ndipo ine—ndipo ine—ine—ine—ine sindikuganiza kuti ziri mwanjira imeneyo, koma ndikungofuna kuti ndikuuzeni inu zomwe Iye ananena. Ndipo inu mukudziwa zimenezo, inueni. “Monga izo zinali mmasiku a Nowa, pamene miyoyo eyiti inapulumuka mmadzi. Miyoyo eyiti kuchokera pa dziko lapansi, kupulumuka m’madzi.”

⁷⁰ Chabwino, inu mukuti, “Oh, mai! Palibe chifukwa chakuti ine ndiziyesetsera.” Izo zikusonyeza kuti mulibe mtundu wa chikhulupiriro umene inu mukuwusowa.

⁷¹ Ngati kuti kudzangokhala—kudzakhale mmodzi, ameneyo ndidzakhala ine, ameni, chifukwa ine ndikukhulupirira. Mukuona? Umo ndi momwe inu mukufunira kuti muzikhulupirira zimenezo, mwaona, “Ndidzakhala ine.” Ndithudi. Ine ndikufuna kumakhala pafupi kwambiri ndi Iye, mwakuti ine kumadziwa kuti Iye akudzanditenga ine pamene Iye akubwera. Ine ndikukhulupirira zimenezo. Ndiko kulondola. Kotero ngati pali... Ngati wina aliyense ati adzawuphonye iwo, ine ndidzakhala ndiri kumeneko, mwa chisomo Chake. Chifukwa, Iye anandilonjeza ine zimenezo, ndipo ine ndikudziwa kuti ndidzatero—ine ndidzakhala kumeneko, chifukwa Iye sangakhoze kunama. Ndipo ine ndikudziwa kuti solo yanga ndi moyo zikuchitira umboni, ndipo ine ndikuyesetsa kukhala moyo tsiku lililonse monga ngati kuti Iye akubwera, kotero ndidza—ndidza—ine ndidzakhala mmodzi ameneyo. Umo ndi momwe iwe umafuna kumamverera, “Ngati kuti kudzakhale eyiti, ine ndidzakhala mmodzi wa eyiti amenewo; ngati ati adzakhale faivi handiredi, ine ndidzakhala mmodzi wa faivi handiredi amenewo. Sindikudziwa za munthu winayo, koma ine ndikufuna kuti ndidzakhale mmodzi wa faivi handiredi amenewo.” Mukuona? Umo ndi momwe inu mukufuna kumakumbukirira. Mukuona?

⁷² Ndipo ngati inu simumakumbukira zimenezo monga choncho, pali chinachake cholakwika ndi chikhulupiriro chanucho. Mukuona? Inu simuli otsimikiza kuti mwapulumutsidwa panobe, ndiye. Inu mukungopenekera zimenezo. Musamachite zimenezo. Chabwino.

⁷³ Ife sitilowa mu Chisindikizo ichi, si choncho? Chabwino. Ine ndikufuna, usiku uliwonse... Ine sindikudziwa ngati inu mungadandaule nane potenga nthawi yanu. Ife tikhoza kutuluka mofulumirirapo. Palibe zambiri ayi...

⁷⁴ Mu kuwulula kwa izi, kwa Zisindikizo izi, kumbukirani, ndiyo kwenikweni ndime imodzi yokha. Yoyamba, ikumanena kulengeza kwa icho, ndime ya 2. Pafupifupi ndemanga zonse, ndi zina zotero, kuwerenga kwa izo, kapena—kapena kuwerenga kwa maganizo awo, ndipo ine ndakhala—ndipo ine ndakhala ndikukhulupirira nthawizonse monga pafupifupi onse a iwo amachitira, kuti wokwera pa kavalo woyamba uja anali—unali mpingo woyambirira. Koma pamene Mzimu Woyera unadzawulula icho, icho chinali mwamtheradi chosiyana kwa zimenezo. Ndipo kotero ndiye, zonse zimene chimachita, chimangowonetsera chimene icho chiri. Ndiyeno ine ndimayesetsa...

⁷⁵ Tsopano, kwa ine, izi ndi zopatulika kwambiri. Ndi chifukwa chake ndiyenera kuyankha mafunso awa. Ndipo tiyeni tizitenge izi, aliyense akudziwa molunjika, ndipo pa matepi, naponso, kuti iwo adzazimvetse tsopano. Mukuona? Ine ndinayesera

kuyankhula kwa kanthawi, usikuuno, pa kuyika maziko, kuti ndiwapangitse anthu...

⁷⁶ Kuthamangira mkati ndi kukankhira mkati, ndipo, inu musamachite zimenezo. Mukuona? Koma, pamene izo zitero, awo ndi anthu. Ndipo mukutentha muno—mkati muno, ndipo inu—ndipo inu ndi osimidwa.

⁷⁷ Koma inu mwakhala muli, abwino kwambiri. Zopambana zomwe ndinayamba ndawawonapo anthu akuchita, mu kachisi, wakhala uli msonkhano uno; ndipo mukumakhala chete, ndipo azimayi akuwatengera ana awo kokawayamwitsa iwo akayamba kulira. Ndipo chirichonse chakhala chiri chabwino kwambiri.

⁷⁸ Koma ndikumayesetsa kuyika maziko a izo mpaka nditamverera kudzoza kwa Mzimu pa ine, kuti ndinene Mawu awa, kuti ndinene zimene zawululidwa kwa ine. Ndiyeno ngati ine ndakhala kuti, penapake, pochita zimenezo, ngati ndalakwitsa pano, ndithudi pano pamaso pa anthu onse Iye adzandikonza ine chimenecho. Ine—ine ndikufuna zimenezo. Ndizo—ndizo... Ine ndikufuna kuti Izo zikhale molondola. Palibe chifukwa chotengera zimene iwe ukungolingalira. Pali chinachake cholondola, ndipo—ndipo tikufuna Chimenecho. Ife tikufuna Mulungu atipatse ife chimene chiri cholondola.

⁷⁹ Kotero tsopano ife tinawatenga awa, okwera awa, pamene iwo akubwera. Kavalo woyamba, tsopano, ndipo ife tikuzindikira kuti ameneyo anali—wotsutsakhristu amene anapita pamenepo. Ndiyeno ife tinapeza, usiku watha, kuti munthu yemweyo amene anapita apo monga wotsutsakhristu, monga kavalo woyera, ife tinamupeza iye ali ndi lupanga, usiku watha, akukwera, ndi kumapha anthu.

⁸⁰ Tsopano, tsopano, nthawizonse pamakhala zathupi ndi zauzimu. Ndipo chifukwa cha Mpingo, ine ndikufuna kufanizitsa, basi ife tisanafike ku kutsegula kwa Chisindikizo ichi.

⁸¹ Chimene, chomwe Iye wandipatsa ine, ine ndachilemba icho apa. Ine ndiri nawo Malemba angapo apa, masamba seveni kapena eyiti a iwo, ndipo pamene ine ndikulozera kwa iwo.

⁸² Zindikirani, ine ndikufuna kupereka choyimira, cha Mpingo, ndi kuzipanga izo kukhala zomveka kwambiri mwakuti inu mukhala okakamizika kuziwona izo. Mukuona?

⁸³ Tsopano, munali mkwatibwi wachibadwa mmunda wa Edeni. Mukukumbukira usiku watha? Mkwatibwi wachibadwa uyo, iye anali wokomamtima wa Adamu, asanakhalebe mkazi wake, chifukwa iye anali asanamudziwebe iye ngati mkazi wake.

⁸⁴ Basi monga Mariya anali mkazi wa Yosefe, koma iye anali asanamudziwe iye. “Iye anapezeka ali ndi mwana.” Mukuona?

⁸⁵ Tsopano, Adamu asanamudziwe mkazi wake, iye anangokhala mkwatibwi kwa iye. Chabwino. Ndipo ife tikupeza

apo kuti Mulungu... Mkaziyo, mkaziyo anagwa mmunda wa Edeni chifukwa iye analephera kugwiritsitsa ku Mawu a Mulungu.

⁸⁶ Tsopano, Iye ankadziwa kuti Satana akanadzamasulidwa pakati pa iwo, kotero Iye anawapatsa iwo—malo oti adzikhala kuseri kwake; kuwamangira iwo linga. Chabwino, pamenepo, ndani amene akanakhoza kudziwa malo abwinoko aliwonse woti akhale otetezeka, kuposa Mulungu, ngati Iye akuyesetsa kusamalira ana Ake Omwe?

⁸⁷ Ngati ine ndimafuna kumusamalira Joseph wanga wamng'ono, chabwino, m'bale, chirichonse... Ndipo ine nkumadziwa kuti moyo wake ukudalira pa icho, bwanji, ndikanati... ndipo ine ndinali wokhoza kuchita icho. Chabwino, ngati konkire ya mapazi forte, yolimbisidwa, ikanakhala—ikanakhala chinthu chimene chikanachita zimenezo, ndicho... Ine ndikanayipanga iyo kukhala mapazi nainte, kuti ndikhale wotsimikiza, ndi zimenezo.

⁸⁸ Ndipo ngati ndingakhoze kuganizira zimenezo pa mwana wanga wamng'ono, (chimene, ngati moyo wake wachivundi ungati utayike, ine ndikukhulupirira kuti mwanayo angapulumsidwe,) kuli mochuluka bwanji, kwa Mulungu, kwa mwana Wake amene angakhale wotayika Kwamuyaya! Kodi Iye angamuyike iye kuseri kwa chiyani? Iye anamuyika iye kuseri kwa Mawu Ake Omwe. Bola ngati uli mu Mawu amenewo, ndiwe wotetezeka. “Ngati mukhala mwa Ine, ndipo Mawu Anga mwa inu, ndiye mungopempha chimene inu mukufuna.” Ndi zimenezotu, Mawu.

⁸⁹ Kotero, Eva anapita kukayenda mmundamo, ndipo iye anakomana ndi serpenti, munthu wokhala ngati wopukutidwa kwambiri. Ndipo mkaziyo... Ndipo iye anayamba... Tsopano, iye anali kumbali inayo. Mulungu amakhala moyo, amawusa, amagwira ntchito mu kudzichepetsa, osati mwanjira ina iliyonse nkomwe. Mukuona? Tsopano, dona wamng'ono, wodzichepetsa akuyenda motsatira pamenepo, ndipo Satana anabwera pamenepo ngati wanzeru, wothyathyalika, munthu wokhala ngati wopukutidwa. Ndipo iye ankafuna kumugulitsa iye dongosolo. Bola ngati...

⁹⁰ Ziribe kanthu kaya Satana anali pafupi bwanji; bola ngati iye amakhala kuseri kwa Mawu awa, iye anali bwino bwino. [M'bale Branham akusisita Baibulo lake—Mkonzi]. Mukuona? Kotero, musiyeni Satana azichita chirichonse chimene iye akufuna; inu mungokhala ndi Mawu. Sizipanga kusiyana pang'ono.

Ngati iye ati, “Bwanji, iwe ukudwala.”

“Ndi mikwingwirima Yake ine ndachiritsidwa.”

“Chabwino, iwe ufa.”

“Iye adzandidzutsa ine kachiwiri. Iye analonjeza zimenezo.”

⁹¹ Mwaona, ingokhalani kuseri kwa Mawu. Ndizo zonse. Khristu anabwerera ku Mawu, Iyemwini. “Kwalembedwa.” Mukuona? Tsopano, zikhalani kuseri kwa Mawu.

⁹² Koma, Eva, anayamba kukhala ngati akulekerera, koma iye sanalekerere iwo wonse. Iye anangolekerera mfundo imodzi yaing’ono yokha. Ndipo ndicho chimene Satana ankafuna kuti iye achite. Iye anamuchotsa iye kuseri kwa lonjezo la Mulungu, polingalira.

Musamayesere konse kulingalira Mawu a Mulungu. Muzingowakhulupirira Iwo! Mukuona?

⁹³ Kotero, iye anatuluka nachoka Kumeneko. Ndipo Adamu asanafike konse kwa iye, kukhala mkazi wake, iye anali ataipitsidwa kale ndi Satana. Ndipo iye. . .

⁹⁴ Ndipo kodi inu munazindikira? Khristu anachita chinthu chomwecho, ndendende. Tsopano, podzawombola, Mulungu ankayenera kukhala pamenepo poyamba. Kodi inu munazindikira? Mariya, iye asanafike kwa Yosefe, Mzimu Woyera unali utafika kale pamenepo. Amen. Mukuona? Apo ndi pamene Muwomboliyo akubwerapo.

⁹⁵ Tsopano, tsopano zindikirani, mkazi wachibadwa anagwa, ndipo Mulungu anapanga njira yoti iye awomboledwere. Ngakhale iye anali atagwa, Iye anapanga njira.

⁹⁶ Tsopano, ameneyo anali mkwatibwi woyamba pa dziko lapansi, anagwa, iye ndi mwamuna wake asanakwatirane. Iye anagwa, mwa—mwa chifukwa cha—cha kulingalira, mmalo mokhala ndi Mawu. Iye anagwa. Ndipo iye anagwera ku imfa, kulekana Kwamuyaya. Limodzi ndi iye, iye anamutenga mwamuna wake ndi china chirichonse chimene chinalipo pa dziko lapansi. Iye anagwa!

⁹⁷ Tsopano, koma, Mulungu, wodzaza ndi chifundo, anapanga njira yoti amuwombolere mkazi ameneyo. Ndipo tsopano Iye anamulonjeza iye, kumuza iye kuti nthawiyina, mtsogolomo, Mawu owona adzabwera kwa iye kachiwiri. Mawu owona adzapangidwa kudziwika kwa iye. Tsopano kumbukirani zimenezo. Chifukwa, Iye analonjeza Khristu, kudzera mwa mkazi.

⁹⁸ Ndipo Khristu ndi Mawu. Yohane Woyera 1, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi,” mwaona, “ndipo anadzakhala nafe.” Mulungu anakhala ndi ife mu thupi. Iye anali Mawu.

⁹⁹ Asanakhale Mawu, limakhala ganizo. Ndipo ganizo limayenera kulengedwa. Chabwino. Kotero, maganizo a Mulungu anadzakhala chirengedwe pamene iwo anayankhulidwa, mwa Mawu. Ndi pamene Iye akuwapereka

iwo kwa—kwa inu ngati ganizo, ganizo Lake, ndipo ilo lawululidwa kwa inu. Ndiye, ilo limakhalabe ganizo mpaka *iwe* utaliyankhula ilo. Ndicho chifukwa chake. . .

¹⁰⁰ Mose anapita kukapemphera. Lawi la Moto lija litamuzinga iye, ndipo Iye anati, “Pita, ukalozetse ndodo yako kummawa, ndipo ukati, ukayitanitse ‘ntchentche.’”

¹⁰¹ Uko kunalibe ntchentche. Koma iye anapita nakalozetsa ndodoyo kumeneko, ndipo anati, “Pakhale ntchentche.” Kunalibe ntchentche nkomwe, apobe. Anabwererakonso kumeneko. Koma mawu, ganizo la Mulungu, linali litayankhulidwa kale. Iwo ndi mawu, tsopano iwo ayenera kuchitika.

¹⁰² Tsopano kodi inu simukuwona pamene Yesu ananena? “Ngati mudzanena kwa phiri ili; osati ngati Ine ndidzanena ilo. Koma *inu* mukadzanena kwa phiri ili, ‘Suntha.’”

¹⁰³ Ndipo chinthu choyambirira, ine ndikuganiza, mu nthawi ya Mose, ntchentche yayikulu yokalamba yagirini inayamba kulira. Ndipo, patapita kanthawi, izo zinalipo mapaundi faivi pa yadi. Mukuona? Kodi izo zinachokera kuti? Iye. . . Mulungu anazilenga izo. Kodi inu simukuona momwe. . .

¹⁰⁴ Mulungu akhoza kuliwononga dzikoli usikuuno, ndi—ndi atongole, ngati Iye atafuna kutero. Chabwino, Iye akhoza kuwaunjika atongole mpaka ku mwezi. Chinthu chokhacho chimene Iye angakhoze kuchita ndicho kungoti, “Pakhale atongole, afike ku mwezi.” Icho chingakhale chonse chimene chingakhale kwa icho. Popanda zosakaniza kapena kanthu kena, iwo angakhale akungochulukira, chulukira, kumachulukirabe. Mukuona?

¹⁰⁵ Iye akhoza kuchita chimene Iye akufuna. Iye ndi Mulungu, Mlengi. Chinthu chokhacho choti achite ndicho kungoyankhula zimenezo. [M’bale Branham anakhwatsitsa zala zake—Mkonzi]. Ndiko kulondola. Iye ndi Mlengi. Tsopano, ngati ife titangofika pozindikira momwe Iye aliri wamkulu! Mukuona? Iye amangochita zimene Iye akufuna.

¹⁰⁶ Iye amakhala pamenepo ndi kumayang’ana pa anthu, ndipo aphunzitsi aang’ono awa, ochuluka nzeru, ndi, “Kulibeko Mulungu,” ndi—ndi chirichonse. Huh! Bwanji, izo ziri basi monga zinachitikira ku Babulo, panonso. Babulo, kani.

¹⁰⁷ Tsopano ife tikuzindikira kuti Mulungu anamuza Eva, kuti, “Pakadzapita nthawi yaitali chomwechi, Mawu adzabwereranso kwa iwe.” Tsopano, kodi iye anagwa bwanji? Ine ndikufuna kuti kalasi yanga inene zimenezo. Kodi iye anagwa kuchokera ku chiyani? Kodi Eva anagwa kuchokera ku chiyani? Mawu. Ndi kulondola kumeneko? Mawu. Ndipo Mulungu anati Iye akanadzapanga njira yoti amuwombolere iye kuti adzabwerere ku Mawu kachiwiri. Chabwino. Pakadzapita nthawi yaitali kwambiri, Mawu akanadzadziwitsidwa kwa

ieye. Chabwino. Mawu akanadzabwera kwa cholinga chimodzi tsopano. Mugwiritsitse tsopano, chimene ine ndikunena. Mawu akanadzabwera kwa iye kwa cholinga chimodzi, icho chinali kwa chiwombolo. Chabwino.

¹⁰⁸ Koma, kufikira—kufikira nthawi imeneyo, iye anali ndi cholowa mmalo chimene chikanati—chimene chikanamagwira ntchito kufikira nthawiyo itafika ya Mawu apachiyambi. Tsopano inu—inu mukumvetsa bwinobwino? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Mukuona? Iye anamuuza iye kuti Mawu akanadzabwera kwa iye kachiwiri, koma, kufikira nthawi imeneyo, Iye anamupatsa iye cholowa mmalo kufikira nthawi imeneyo itadzafika. Kotero, Iye anamupatsa iye nsembe yoti azipanga, cholowa mmalo mwa Magazi amenewo.

¹⁰⁹ Tsopano, magaziwo anali a ng’ombe ndi nkhoa, ndi mbuzi ndi zinthu, koma iwo sankachotsa tchimo lake. Mukuona? Iwo ankangophimba tchimo lake. Iwo sankalichotsapo ilo, nkomwe. Iwo ankalphimba ilo. Pakuti, iwo anali magazi a chinyama, ndipo mmagazi a chinyama mumakhala moyo wa chinyama. Iwo anali cholowa mmalo kufikira chenichenicho . . . Tsopano valani zikhotho zanu.

¹¹⁰ Magazi enieni, a munthu, monga anthu akanadzakhala, atadasandulika thupi (Mulungu); popanda kugonana, namwali, kubadwa kwa namwali kunapereka chimenecho. Tsopano Mawu a Mulungu, lonjezo, anadzakhala Magazi, ndipo anadzakhala mu thupi la Umunthu wa Yesu Khristu Mpulumutsi. “Magazi a ng’ombe ndi mbuzi, ndi zina zotero . . .”

¹¹¹ Koma tsopano dikirani. Apa Mulungu anapanga lonjezo, kunena kuti zidzakhala pamenepo pamene Iwo adzabwere, “Mbewu yake iyenera idzavulaze mutu wa serpenti.” Tsopano, ngati mbewu yake ikanangobwera monga kuchokera kwa Adamu, kapena monga ikanachokera kwa serpenti, ndi zina zotero, ndiye iyo ikanadzakhala mbewu yochimwa.

¹¹² Ndi chifukwa chake Yohane analira. Uko kunalibe munthu, chifukwa palibe munthu . . . Aliyense anali atawolokera, mbali inayo ya dzenje, phompho. Koma ikanadzabwera nthawi pamene magazi olova mmalo awa a zinyama akanati adzathetsedwe, pamene enieni, Magazi okhala mu thupi anabwera: Mulungu, atapangidwa mnofu ndi Magazi. Baibulo linati Iye anali. Timoteo Woyamba 3:16, “Popanda kutsutsana chachikulu ndi chinsinsi cha umulungu: pakuti Mulungu anawonetseredwa mu thupi.” Ndiko kulondola. Kubadwa kwa namwali kunachita izi.

¹¹³ Tsopano, magazi a nkhoa ndi mbuzi ankaphimba tchimo, koma iwo sankalichotsa ilo, pakuti iwo anali magazi a chinyama. Koma iwo anali oti akhale abwino bwino, anali oti akhale cholowa mmalo.

114 Ndipo iwo ndithudi anafika—anafika pozolowera cholowa mmalo chimenecho, ndipo kotero iwo ankangopitirirabe.

115 Ndipo, pamene, Mawu enieni, olonjezedwa anadzawonetseredwa mwa Yesu Khristu, Yemwe anatsimikizira kukhala Mwana wa Mlengi wamkulu, Mulungu; ndipo anatsimikiziridwa, Iyemwini, pokhala Mawu amoyo a Mulungu. Psyii! Mai! Iye anatsimikizira kuti Iye anali. Iye ankakhoza kuyankhula zinthu nkukhalapo.

116 Palibe munthu, kapena—kapena palibe kanthu mdziko, kakanakhoza kuchita zimenezo. Palibe chinthu pa dziko lapansi chimene chingakhoze kulenga, koma Mulungu. Mdierekezi sangakhoze kulenga. Iye ndi wopotoza wa chimene chalengedwa kale, koma iye sangakhoze kulenga. Tchimo ndi chirungamo chabe chopotozedwa. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza. Bodza ndi chiyani? Ndi choonadi choyankhulidwa mokhota. Mukuona? Chigololo ndi chiyani? Kachitidwe kolondola kololezedwa katapotozedwa. Chirichonse mu tchimo, tchimo ndi Choonadi basi chopotozedwa. Tsopano, iye sakanakhoza kulenga.

117 Koma pamene Khristu anadzabwera, anadzatsimikizira kuti Iye anali Mlengi. Apo panali Magazi amene anali atalonjezedwa. Tsopano ngati inu mukufuna kuti muwerenge zimenezo, inu... Tiyeni tingotsegula kwa miniti chabe. Ife titenga nthawi pa izi, mulimonse, usikuuno. Ine...

118 Izo zimandipangitsa ine manjenje. Ine ndikuganiza kuti aliyense akufuna kuti azipita kwawo, inu mukudziwa. Ndipo kotero ndizo... [Osonkhana akuti, “Ayi.”—Mkonzi]. Tsopano tiyeni tipeze Machitidwe 2. Zikomo inu. Ndipo ife tingo...

119 Machitidwe 2, ndipo ife tipeza ngati izi ziri zolondola, kapena ayi, ngati Iye anatsimikiziridwa kuti Iye anali Mulungu. Chabwino. Tipeze Machitidwe 2. Tsopano tiyeni tifique apa pa ndime ya 22, Petro akuyankhula, pa Tsiku la Pentekoste.

Amuna inu a mu Israeli, mverani mawu awa; Yesu waku Nazareti, mwamuna wotsimikiziridwa ndi Mulungu pakati panu mwa zozizwitsa... zodabwitsa ndi chizindikiro, zimene Mulungu anazichita mwa iye pakati panu, monga inu wanu... al-... inu eniakenso mukudziwa:

120 “Mwamuna amene anatsimikiziridwa, kuti anali Mulungu pakati panu.” Mwa zinthu zomwezo zimene Iye anazichita, anatsimikizira kuti Iye anali. Apa pali Petro, ataimirira pa Sanhedrin, akuwauza iwo.

121 Nikodemo ankadziwa chimodzimodzi. Iye anati, “Rabbi, ife tonse timadziwa kuti Inu ndinu Mphunzitsi wochokera kwa Mulungu, chifukwa palibe munthu amene angakhoze kuchita zinthu izi pokhapokha Iye atachokera kwa Mulungu.” Mukuona? Iwo ankadziwa zimenezo. Koma bwanji?

122 Tsopano penyani. Tsopano, Eva analonjezedwa ichi. Koma pamene... Mkwatibwi ameneyo anabwera mpaka mmusi, ndipo anakana, pamene Mawu enieni anadzabwera kwa iye. Kotero, mkaziyo anakana kuti azindikire; mkwatibwi Wachihebri. Pakuti, iye anali mkwatibwi wa—wa Mulungu; Iye anamusiya iye, mwa chilekano. Nkulondola uko? Iye anali mkwatibwi wa Mulungu.

123 Inu mukuti, “Chabwino, iwo anali asanakwatirane konse apobe.” Uko nkulondola. Koma Yosefe anamusiya Mariya asanati... Anali woti amusudzule Mariya iwo asanakwatirane. Mukuona? Iye anatomeredwa kwa iye.

124 Ndipo pamene Iye anabwera, ndipo Mawu amene Iye anawalonjeza, atabwerera chikwati, Iye anamupeza iye atakutidwa mu zolowa mmalo zake, moyipa kwambiri, mwakuti iye sakanatenga lonjezo lenileni limene linali litapangidwa, Mawu, Khristu.

125 Mwinamwake inu simukumvetsa zimenezo. Tsopano ndiroleni ine ndibwereze zimenezo kachiwiri. Ine ndikufuna kuti inu mumvetsetse izi, mwaona.

126 Iye anali atalonjezedwa, (mkwatibwi, Eva), kuti kukanadzakhala Muwomboli. Muwomboli wake akanadzakhala Mawu. Ndipo pamene Mawu anabwera, atapangidwa thupi, iye anawakana Iwo. Iye anapatsidwa zolowa mmalo. Tsopano gwirani chimenecho, “cholowa mmalo.” Anapatsidwa zolowa mmalo kuti azipitirirabe, kufikira Muwomboliyo atadzabwera. Ndipo pamene Muwomboliyo anabwera, iye ankafuna kuti azipitirira ndi cholowa mmalo chakecho, ndipo anawakana Mawu owona. Mukuwona zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndipo ameneyo anali mkwatibwi wa Chihebri.

127 Momwemonso anachita Iye, mwa Eva wachiwiri, mkwatibwi, mayi wa zamoyo zonse zauzimu. Mukuona? *Eva* amatanthauza “mayi wa onse,” omwe ali mzimu... “onse amoyo.” *Eva*, “mayi wa onse amene ali amoyo.”

128 Tsopano, ndipo pamene Iye anabwera kwa mkwatibwi wa Chihebri, iye anali mayi wa onse amene anali amoyo, koma iye anawakana Iwo.

129 Eva wachibadwa anagwa, mu Edeni, pa kumvetsera ku kulingalira kwa Satana motsutsa Mawu a Mulungu. Umo ndi momwe iye anagwera. Chabwino, bwana. Iye anagwa chifukwa anachita zimenezo.

130 Eva Wauzimu, tsopano, ndiwo mpingo, mkwatibwi wa Khristu. Iye anagwa, osati mu Edeni, koma mu Roma, mwaona, ku Msonkhano wa Nicaea, pamene iye anakana, mpingo wa Chipentekoste uja, umene unapita mpaka ku Nicaea, ndi kukamvetsera ku kulingalira kwa Roma, mmalo mogwiritsitsa ku Mawu, iye anagwa. Ndipo chirichonse cha kutali kwa

ieye, chinafa naye iye, chomuzungulira iye. Tsopano, basi monga momwe Eva wachibadwa anagwera, momwemonso Eva wauzimu anagwa. Mkwatibwi wa Mulungu anagwa—anagwa mmunda; Mkwatibwi wa Khristu anagwa mu Roma. Mukuona?

¹³¹ Zindikirani, mwa kulingalira komweko, motsutsa Mawu a Mulungu, iye nayenso anapinyolitsa maufulu ake a ukoma, kwa Satana. Zomwe, tinazipeza mu kumatula kwa Zisindikizo izi, kuti ameneyo anali Satana, ndipo akadali Satana kumeneko. Baibulo linati ndi mpando kumene wa Satana. Ndipo monga Eva anapinyolitsa—maufulu ake a ukoma, ndi kuwapereka iwo kwa Satana, mmunda wa Edeni; mpingo, mkwatibwi wa Khristu, anachita chinthu chomwecho ku Roma, pamene iwo anapinyolitsa Baibulo ndikukatenga miyambo ndi zolingalira zawo. Mukuona momwe zikukhalira choimira?

¹³² Inu mukangofanizitsa zoimira zimenezo, inu mukhala okakamizika kutulukamo bwino bwino. Ngati dzanja langa likuwoneka ngati... Ngati sindinadziwonapo ndekha konse, ndipo ine nkuwona mthunzi wanga ukubwera, ine ndingadziwe basi pafupifupi momwe ine ndimawonekera. Mukuona? Koma, ndiyo njira yake. Ngati inu mukufuna kuwona chimene chikubwera, muyang'ane chimene chakhala chiripo. “Pakuti zi... zinthu zonse zakale zinali mithunzi ya zinthu zakudza,” Baibulo linatero. Chabwino.

¹³³ Pakuti, iye anapinyolitsa Mawu ake aukoma, Mawu a Mulungu, pamene anagulitsa Baibulo, ndi kuikamo munthu mmenemo amene amanena kuti mpingo uli nawo maufulu osintha chirichonse chimene iwo akufuna kusintha. Ndipo iwo azichita zimenezo. Ndipo mkwatibwi wa Khristu, mkwatibwi wa chipentekoste, anagulitsa ukoma wake, pa Nicaea, basi monga momwe Eva anagulitsira ukoma wake kwa Satana mmunda wa Edeni. Ndendende. Chabwino.

¹³⁴ Mulungu walonjeza; mpingo uno, mpingo wa chipentekoste uwu, podziwa kuti iwo ukanadzachita zimenezo; monga Iye anachitira kwa Eva, Mulungu walonjeza.

¹³⁵ Mpingo wa chipentekoste, kodi inu mukukhulupirira kuti iwo unagulitsa maufulu ake obadwa nawo, usanati... ukoma wake, pamene iwo unachoka cha kumeneko? Inu mukukhulupirira zimenezo? Iwo, ndithudi, iwo unatero. Ndiye ndi kaubwino wanji kachikhulupiriro, kosakhazikika pa Baibulo ili? Ine ndikufuna wina apezze chimene chimatchedwa Kachikhulupiriro ka Atumwi, kapena ngakhale liwu limodzi la iko mu Baibulo. Ako ndi kachikhulupiriro ka Chikatolika, osati chikhulupiriro cha atumwi.

¹³⁶ Mukawerenge Machitidwe 2:38, ndiko Kachikhulupiriro ka atumwi, ngati iye ali nako kalikonse...?... Tsopano, ndicho chimene iwo ankachigwiritsa ntchito nthawi zonse, mulimonse. Kotero ngati inu... Mukuona?

¹³⁷ Kotero, iwo anagulitsa maufulu awo obadwa nawo. Osati kokha zokhazo, Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Achipentekoste, ena onse a iwo, achita zomwezo. Iye anapanga chipembedzo. Roma, chimene chinamupangitsa iye kuchita zimenezo, iye anapanga chipembedzo ndipo anamuyika munthu pa ulamuliro wa icho. Ndipo Amethodisti, Abaptisti, Achipentekoste ndi aliwonsewo, achita chinthu chomwecho, ayika gulu la anthu pa ulamuliro wa icho. Ziribe kanthu chimene Mulungu akunena, iwo... Iwe umayenera kuchita izo mwanjira yomwe iwo akuti uchitire izo.

¹³⁸ Chabwino, ndi chiyani chimenecho? Si kanthu mdziko koma uhule wauzimu, mkazi wa mtundu wolakwika; inde, bwana, tizikhulupiriro, tizikhulupiriro tabodza, topangidwa ndi anthu. Ndiye iye anadzakhala, pamene iye anachita zimenezo... Tsopano ine nditsimikizira izi. Iye anadzakhala hule, kwa Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira kuti Baibulo limanena zimenezo? Inde, bwana. Ana ake aakazi achita zomwezo.

¹³⁹ Tsopano mu Chivumbulutso 17, ngati inu mukufuna kulemba zimenezo. Yohane anatengedwera mu Mzimu, “Ndipo anawona hule wamkulu atakhala pa...” Ndipo ife tinawerenga zimenezo usiku wathawu. Ndipo apo panali mapiri asanu ndi awiri, ndipo ndendende chimene iye anali atachita. Ndipo iye anali atalipatsa dziko lapansi ziwerewere zake zauve. Nkulondola uko? “Ndipo mafumu onse a mdziko lapansi anachita naye iye chiwerewere,” chinyengo, ndi kuba, ndi kunama, ndi kulipiritsa kulapa, ndi—ndi kudzitunduzi, ndi chinthu china chirichonse.

¹⁴⁰ Chabwino, tsopano kumbukirani, iye anali ndi ana aakazi. Chabwino, ngati iye anali atakhala gulu, ndipo ali pansu pa kachitidwe ka bungwe, ndiye kachitidwe konseko ndi kolakwika. Ndipo ngati Eva, posamumvera Mulungu, anaponyera chirichonse ku imfa, chimene chinali pansu pa iye; ndipo mpingo uliwonse umene upanga bungwe, umaponyera chirichonse ku imfa, pansu pa iwo. Ndendende. Chinthu chonsecho chapita. Ndizo ndendende molingana ndi Mawu apa. Werengani Chivumbulutso 17. Ndipo Baibulo linanena kuti Iye “akanadzamuwotcha iye ndi moto, ndi ana ake onse limodzi ndi iye.” Ndiko kulondola. Zimenezo zikutanthauza, kachitidwe kalikonse ka bungwe kadzawotchedwa, limodzi ndi huleyo.

¹⁴¹ Tsopano, izo zikumveka mosanyengerera, ndipo ine—ine ndikudziwa kuti inu mudzamva kuchokera kwa iyo, ndipo ine—ine ndikufuna kuti ndikamvetsere kwa iyo. Ndipo ine—ine... Ndiko kulondola, chonchobe. Baibulo linanena chomwecho, kotero izo zikupangitsa izo kukhala zolondola.

¹⁴² Iye anadzakhala “hule.” Inu mukhoza kuziwerenga izo mu Chivumbulutso, mutu wa 17. Iye, kodi iye anachita chiyani? Iye anachita ziwerewere, motsutsana naye Mwamuna wake

yemwe. “Chabwino,” inu mukuti, “ayi, ndiro Baibulo.” Mawu ndi Mulungu. Ndipo ngati inu mutenga kanthu kamodzi. . .

143 Kodi inu mungafune kuti mkazi wanu azipsyopsyonana ndi mwamuna wina? Ngati iye sanachite zoposa zimenezo, inu simungafune kuti iye azichita zimenezo. Iye angatsimikizire kubalalika-kwake.

144 “Aliyense amene adzachotse Liwu limodzi kuchokera mwa Ilo, kapena kuwonjezera limodzi kwa Ilo.” Aleluya! Khristu akufuna kuti Mkazi Wake akhale wangwiro ndi Mawu. Umo ndi momwe Iye ayenera kukhalira.

145 Chifukwa, palibe kanthu, ngakhale dontho limodzi, kapena kukhwatsha kumodzi, kapena kalikonse, kapena neno, zidzachoke kwa lamulo limenelo, kapena kuchokera ku Bukhu limenelo, kufikira Izo zonse zitakwaniritsidwa. Yesu anati, “Zonse kumwamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu Anga sadzachoka konse.”

146 Musayike kutanthauzira kwanukwanu kulikonse kwa Iwo. Iye akufuna angwiro, osakhudzidwa, opanda ngakhale kudzivula. Ine sindingafune kuti mkazi wanga azinyengana ndi mwamuna wina. Ndipo pamene inu muyamba kumamvetsera ku mtundu uliwonse wa malingaliro, osakhala Iwo, inu mukumvetsera, inu mukunyengana naye Satana. Amen! Kodi izo sizikukupangitsani inu kumverera mwachipembedzo? Mulungu akufuna kuti inu mukhale osakhudzidwa. Mukhale pomwepo ndi Mawu amenewo. Mukhale pomwepo ndi Iwo. Chabwino.

147 Mulungu analonjeza kwa iye, monga Iye anachitira kwa Eva mmunda wa Edeni, kwa Eva wotsiriza uyu apa. Amene, mpingo wa chipentekoste, chiyambi cha mpingo, mpingo iwowomwe, ndi mayi wa anthu onse amoyo, chifukwa, malingana ngati iwo akupita mmenemo. Koma, inu mukuona, pamene iwo atenga machimo ake, iwo amafa limodzi naye.

148 Apa pakubwera mnyamata wamng’ono pamenepo. Iye akuti, “Ine—ine ndikufuna kuti ndizimutumikira Mulungu.”

149 Iwo amati, “Chabwino, apa pali chimene iwe uchite. Pita kumusi uko ndipo ukalape.”

“Chabwino, ine ndikachita zimenezo. Ulemelero kwa Mulungu!” Pita kumusi uko, ukalape.

150 “Tsopano bwera udzatiwowine ife.” Apo, ndi zimenezotu pamenepo. Uh-huh. Mukuona? Icho chinachita zimenezo. Huh! Ndiko kulondola, anafa nazo izo kumene. Mukuona? Mukuona? Ndizo basi. . . Ndicho chimene Bukhu ili likuphunzitsa, mwaona, osati zimene ine ndikunena. Chifukwa, Ilo likutero Apa, chotero. Chabwino.

151 Tsopano, Mulungu wamulonjeza iye, monga Iye anachitira kwa Eva. Iye anamuza Eva kuti pakanadzabwera nthawi

imene—Mawu akanadzabwereranso kwa iye kachiwiri. Tsopano inu mukukumbukira zimenezo? Chimene iye anachitaya, chikanadzabwezeretsedwa. Chifukwa, pali Chinthu chimodzi chokha chimene chingakhoze kubwezeretsa, ndipo ndicho Mawu. Ndendende.

¹⁵² Ine ndinati, kuwombera mfuti; ngati iwe sumenya pa chandamale, upeze pamene iyo inaphonya. Iwe uyenera kubwerera mmbuyo pamenepo ndi kukayambiranso kachiwiri. Mukuona?

¹⁵³ Ndipo ngati ubwerera, iwe upite ku Nicaea. Ndi kumene ukayambire kachiwiri, mwaona. Ubwerere mmbuyo, kutali kutalikirana nawo mabungwe amenewo, kutali ndi mipingo yonse iyo. Ndipo ife takhala tikuziwona Zisindikizo izi mwangwiro basi.

¹⁵⁴ Ine nthawizonse ndakhala ndikudabwa, moyo wanga wonse, chifukwa chimene ine ndinali kutsutsa kwambiri machitidwe a bungwe. Osati anthuwo, ayi. Anthuwo ali basi ngati ine kapena inu, kapena wina aliyenseyo. Koma kachitidwe kameneko, kachitidwe kachipembedzo ako, tsopano ine ndikuziwona izo pomwepa apa. Ine sindimazidziwa izo kufikira tsopano. Ndipo uko nkulondola.

¹⁵⁵ Mulungu anamulonjeza Eva wauzimu, chimodzimodzi monga Iye anachitira ndi Eva wachibadwa, kuti Mawu akanadzabwezeretsedwa kwa iye kachiwiri. Mmasiku otsiriza Iye akanadzawubwezeretsa Mpingo, ku Mawu apachiyambi kachiwiri.

¹⁵⁶ Tsopano penyani mwatcheru kwenikweni. Ine—ine ndikufuna kuti inu mukhale otsimikiza tsopano. Mulungu anamulonjeza Eva, kuti nthawi ikanadzabwera pamene Mawu akanati adzabwezeretsedwe ndi Mbewu yake. Mawu awa, Pawokha, akanadzakhala Mbewu. Ndipo pamene iwo anamupatsa iye cholowa mmalo, iye anagwira cholowa mmalo chimenecho. Ndipo pamene Mawu anabwera kwa iye, kodi iye anachita chiyani? “Ine sindikuwafuna iwo.” Iwo anali odzichepetsa kwambiri. Sanawoneke mwabwino, kwa iye. Sanali opukutidwa mokwanira. “Khola? Oh, mai! Mai! Munthu wonga ameneyo, sanapiteko tsiku limodzi ku sukulu? Chabwino, Ine sindingakhoze kulandira zimenezo. Ameneyo si Mesiya. Munthu womawalola anyamata azimuseweretsa iye monga chomwecho, ndiyeno nkumamutcha iye ‘Mesiya’? Kuwalola iwo kumuyika chisanza pa nkhope yake, kenako nkudzamumenya iye pa mutu? Ndipo anadzitcha yekha Mneneri, Mneneri weniweni, atawuka?”

¹⁵⁷ Kwenikweni, iwo sankawadziwa aneneri. Yesu ananena chomwecho. Iye anati, “Ngati inu mukanawadziwa aneneri, inu mukanandidziwa Ine.” Ndiko kulondola.

¹⁵⁸ Tsopano zindikirani. Koma pamene Mawu anabwera kwa iye, mwanjira, ndendende basi momwe Mulungu ananenera kuti Iwo akanadzabwerera; iye anali atawalingalira Iwo mwanjira ina yake. Ine ndikuyankhula za mkwatibwi, mkwatibwi wa Chiyuda, mkwatibwi wa Chihebri. Ameneyo anali Eva, kuyamba ndi kuyamba. Ndiye pamene Iwo anatulukira apa, iye sanawafune Iwo. Iye ankafuna kuti azikhalabe ndi zolowa mmalo zake.

¹⁵⁹ Tsopano, Mulungu anamulonjeza Eva wauzimu, pa Pentekoste, anachinena icho ngakhale icho chisanachitike, zaka foro handiredi mpingo usanagwe konse, kuti iwo akanadzagwera kutali, ndipo iwo akanadzachita zimene iwo anachita. Koma, Iye analonjeza, kuti mmasiku otsiriza Iye akanadzatumiza Mawu kachiwiri.

¹⁶⁰ Yesu anayankhula chinthu chomwecho pamene Iye anali pa dziko lapansi; Iye akanadzawatumiza Iwo kachiwiri. Ndipo kodi icho... Kodi Iwo adzapeza chiyani? Iwo adzapeza chinthu chomwecho chimene Iwo anachipeza pamene Iwo anabwera koyamba. Kulondola. Iwo ali nazo... Iwo, iwo akufuna zolowa mmalo zawo. Iwo akufuna chipembedzo chawo. Iwo akufuna tizikhulupiriro tawo. Iwo akufuna kuti azikhala moyo basi momwe iwo akufuna kumakhala. Ndipo iwo akufuna, “Chabwino, ine ndine *Wakuti-ndi-wakuti*. Ine ndine wa *Chakuti-ndi-chakuti*.” Sizimapanga kusi yana kulikonse chimene Mulungu akuchita, mochuluka momwe Iye akudziwonetserera Yekha; Iye akhoza kuwukitsa akufa; Iye akhoza kunena zinsinsi za mmitima; Iye akhoza kuchita chirichonse chimene Baibulo linati Iye akanadzachichita. Zimenezo sizimapanga kusi yana mpang’ono pomwe. “Ngati izo siziri zolumikizana ndi bungwe langa, palibe kanthu kwa Izo.” Mukuona?

¹⁶¹ Chinthu chomwecho chimene mkwatibwi wa Chihebri anachita, ndiko kulondola, mwaona, iwo anamvetsera kwa cholowa mmalo chawo. Ndipo Mulungu anawalonjeza iwo zenizeni. Ndipo pamene chenicheni chinabwera, iwo sanachifune Ichu. Ichu chinali chodzichepetsa kwambiri.

¹⁶² Tsopano ndi chinthu chomwecho lero, pamene—pamene Ichu chiwuka powonekera. Tsopano, Mulungu anati, mu Malaki 4, kuti Iye akanadzatumiza Uthenga mmasiku otsiriza, umene ukanati udzabwezeretse. Yoweli anati, “Ine ndidzabwezeretsa zaka zonse.” Chirichonse chimene Roma anadya, ndi chirichonse chimene Amethodisti anadya, ndi chirichonse chimene Abaptisti anadya, kuchokera pa nthambi yapachiyambi ya chipentekoste ija, Mulungu anati, “Ine ndidzabwezeretsa mu tsiku lotsiriza.” Ndiko kulondola.

¹⁶³ Ndipo Iye akhoza kutitumizira ife munthu woteroyo amene ati adzakhale... Chinthu chokhacho chimene Mulungu

anatumizako konse Mawu Ake chinali mneneri, osati kwa okonzanso; kwa aneneri. Ilo silinali ora la izo. Tsopano ndi... zikufika kukhala oralo, ndipo ndi chifukwa chake ife tikuyang'anira icho kuti chibwere. Ichu chidzakhala chodzichepetsa kwambiri ndi chodekha! Ndipo chotero... Oh, mai!

¹⁶⁴ Inu mukuganiza kuti Amethodisti olemkezeka amenewo, Abaptisti, ndi Apresbateria, Achipentekoste, adzachilandira konse chimenecho?

"Oh," inu mukuti, "Achipentekoste?"

¹⁶⁵ Achipentekoste ndi a Laodikaya. "Olemera, ndipo osasowa kanthu."

¹⁶⁶ Ilo linati, "Iwe sukudziwa kuti ndiwe wosauka." Ukhoza kukhala ukumanga manyumba amadola mamillionsi, koma ndiwe wosaukabe, kusauka mwauzimu.

"Oh," iwe ukuti, "Ine ndikuziwona Izo zonse."

"Ndiwe wakhungu!"

"Chabwino," iwe ukuti, "Mulungu adalitsike, ine ndavala."

"Wamaliseche!"

"Chabwino, ine ndiri wotsimikiza za anyamata athu. Ife tiri nawo maseminare. Ife..."

¹⁶⁷ "Ndipo sukudziwa zimenezo." Tsopano izo ziri basi motsemphanitsa. Tsopano, ngati Baibulo linanena kuti Mpingo wa Laodikaya ukanadzakhala mu chikhalidwe chimenecho...

¹⁶⁸ Ndipo palibe munthu padziko lapansi angakhoze kukana kuti uwu si m'badwo wotsiriza, chifukwa, M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya, kapena, m'badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri. Ndipo, apa ife tiri, zaka thuu sauzande zachiwiri zikutsirizitsa iwo. Kulibenso mibadwo ina ya mpingo. Ndi chifukwa chake inu abale a Mvula ya Masika simukanakhoza kuyambitsa bungwe lina. Sikudzakhalanso wina. Uko nkulondola. Iwo uli pamapeto. Amen. Sikungakhoze kukhalanso mibadwo ina ya mpingo. Iyo yonse yatha.

¹⁶⁹ Koma ndiye ngati uthenga wa chipentekoste unali uthenga wotsiriza... Chimene, kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, mauthenga atatu otsirizawo, mibadwo itatu yotsiriza ya mpingo ikupanga Kubadwa kwathunthu.

¹⁷⁰ Basi monga pamene mkazi akukhala, ali woti abereke mwana wake; chinthu chenicheni choyambirira chimene chimachitika ndicho madzi, chinthu chotsatira ndi magazi, chinthu chotsatira ndi moyo.

¹⁷¹ Pamene anamupha Yesu pa mtanda, zinthu zinatuluka mthupi Lake, kuti zikapange kwatsopano... kuti zikapange—Kubadwa. Iwo anakantha kumbali Yake, Magazi ndi madzi zinatuluka, ndipo, "Mmanja Mwanu Ine ndikupereka Mzimu

Wanga.” Chimene chinabwera kuchokera mu thupi Lake chinali madzi, Magazi, Mzimu.

¹⁷² Tsopano, Yohane Woyamba 5:7 amakuuzani inu za zimenezo, “Pali atatu amene amachitira umboni Kumwamba, Atate, Mawu (amene ali Khristu,) ndi Mzimu Woyera.” Ndipo atatu awa amagwirizana mu chimodzi; iwo siali mmodzi, koma iwo amagwirizana mu chimodzi. Ndipo alipo atatu amene amachitira umboni... Kapena, “Iwo ndi mmodzi,” ine ndikutanthauza. Ine ndinalakwitsa pamenepo. “Ndipo zitatu zomwe zimachitira umboni mdziko lapansi, ndizo madzi, Magazi, ndi Mzimu, ndipo izo zimagwirizana mu chimodzi.”

¹⁷³ Iwe ukhoza kuyeretsedwa wopanda kulungamitsidwa. Ndipo ukhoza kulungamitsidwa wopanda kuyeretsedwa. Iwe ukhoza kuyeretsedwa wopanda kulandira Mzimu Woyera. Ndizo ndendende.

¹⁷⁴ Ophunzira, mu Yohane 17:17, anayeretsedwa ndipo anapatsidwa mphamvu kuti akatulutse ziwanda, komabe anali alibe Mzimu Woyera. Mukuona? Ndithudi. Ankayenera kupita uko ku Pentekoste, ndi kukayembekezera mpaka Mzimu Woyera utabwera.

¹⁷⁵ Apo ndi pamene Yudasi anawonetsera mawanga ake. Mukuona momwe mzimu umenewo unadutsira kupyola mu kulungamitsidwa, kuyeretsedwa? Koma pamene izo zinafika ku mapeto, iye anawonetsera mawanga ake. Mukuona? Ndiko kulondola.

¹⁷⁶ Tsopano zindikirani, tsopano, ndipo apa ife tiri pa nthawi yotsiriza. Ndipo Eva wauzimu, basi monga... monga Eva Wachihebri analonjezedwa, mkwatibwi wa Chihebri analonjezedwa kuti Mawu adzabwerera. Ndipo mkwatibwi wauzimu kuchokera pa Pentekoste, pamene iye anagwa ku Nicaea, ndiye iye walonjezedwa mmasiku otsiriza kuti Mawu adzabwera kachiwiri. Tsopano inu mukuti, ndiye...

¹⁷⁷ Inu mukufuna Lemba lina, mutenge cha apa, Chivumbulutso 10. Ndipo anati, “Mu ora, nthawi ya—mngelo wotsiriza, mngelo wachisanu ndi chiwiri (wamthenga wachisanu ndi chiwiri) akadzayamba kuwomba, chinsinsi cha Mulungu chidzatsirizika.” Mukuona? Kubwezeretsa kubwerera ku Mawu! Baibulo linati wamthenga uyu wa mmasiku otsiriza akanadzakhala, “Akanadzawabwezeretsa iwo ku Chikhulupiro chapachiyambi kachiwiri, kubwerera ku Chikhulupiro cha atate.” Koma kodi inu mukuganiza kuti iwo adzachilandira Icho? Ayi, bwana. “Mmasiku otsiriza, Iye akanadzabwezeretsa Mawu apachiyambi kachiwiri,” monga Iye ananenera mu Malaki 4.

¹⁷⁸ Koma iye anali atawapinyolitsa. Tsopano, iye anali atawapinyolitsa Mawu amenewo ku Nicaea. Eva anawapinyolitsa mu Edeni; Eva anawakana ake pa Kalvare.

Ndipo gulu la Nicaea likuwakana Iwo mmasiku otsiriza, chimodzimodzi basi. Mai!

¹⁷⁹ Koma pamene Mawu anadza mu thupi la munthu, iyeyo, Eva, mpingo wa Chihebri, mayi wa onse amoyo auzimu panthawiyo, iye anawakana Iwo. Iye anali atafa kwambiri, mu miyambo yake ndi ziphunzitso, mwakuti iye anawaphonya Iwo. Momwemonso watero uyu, ndendende. Chabwino.

¹⁸⁰ Iwo akumuphonya Iye, Mawu amoyo owonetseredwa mthupi, mwa Mawu amene analonjezedwa. Mawu analonjeza kuti akanadzachita zinthu izi. Lonjezo linapangidwa, kuti izo zidzakhala monga chonchi mmasiku otsiriza. “Monga izo zinali mmasiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala mu Kudza kwa Mwana wa munthu.” Tsopano penyani chimene chinachitika ku Sodomu. “Monga zinali mmasiku a Nowa, kotero izo zidzakhalanso mu kudza kwa Mwana wa munthu.” Mukuona? Yang’anani zomwe zinachitika kumeneko. Mukuona? Tsopano, Iye anati icho chikanadzakhala chinthu chomwecho, ndipo ife tikukhala mu tsiku limenelo. Chabwino, ndipo izo zikhoza kukhala, ine ndikuganiza, ine ndikhoza kutenga malonjezo sikisi handiredi a iwo monga choncho, kuchokera mu Lemba, kumangolozera kwa iwo. Mukuona? Tsopano, koma, iwo amawakana Iwo.

¹⁸¹ Iye anagwiritsitsa ku miyambo ndi zolowa mmalo, mmalo mwa—a...Iye anagwiritsitsa ku magari olova mmalo, mmalo mwa Magazi enieniwo. Yesu, Mawu, anatero, pamene Iwo anawonetseredwa kwa iye, “Chifukwa iye anagwiritsitsa ku miyambo iyi...” Yesu, Mawu owonetseredwa, anati kwa mkwatibwi, mkwatibwi wa Chihebri, “Chifukwa iwe wagwira miyambo yako, ukuwapangitsa Mawu a Mulungu kukhala opanda mphamvu kwa iwe. Iwo sangakhoze kukhala amphamvu.”

¹⁸² Tsopano ndi chifukwa chake lero, kuti, zi—zitsitsimutso zimene ife tikuyenera kukhala nazo, ife tiri ndi zitsitsimutso zachipembedzo. Ife sitinakhale nako kukondoweza kwenikweini. Ayi, ayi, ayi. Ayi, bwana. Sindikuganiza kuti ife tiri nazo zitsitsimutso. Ife tiribe. Oh, iwo ali nawo mamillioni ndi mamillioni ndi mamillioni a mamembala a mpingo, koma osati chitsitsimutso paliponse. Ayi. Ayi.

¹⁸³ A—Mkwatibwi sanakhale nacho chitsitsimutso panobe. Mukuona? Kwakhala kulibe chitsitsimutso kumeneko, kulibe mawonetseredwe a Mulungu kuti amukondoweze Mkwatibwi panobe. Mukuona? Ife tikuyembekezera chimenecho tsopano. Zidzatengera Mabingu asanu ndi awiri osadziwika amenewo kumbuyo uko, kuti adzamudzutse Iye kachiwiri, mwaona. Eya. Iye adzawatumiza iwo. Iye analonjeza zimenezo. Tsopano penyani.

¹⁸⁴ Tsopano, iye anali—iye anali wakufa. Ndipo tsopano ngati mipingo ikanaiwala tizikhulupiriro tawo, ndi kuyiwala miyambo yawo, ndi kungotenga Baibulo, kuvomereza lonjezo, ndiye iwo akanakhala amphamvu kwa iwo. Koma, mwaona, Yesu anati, “Inu, ndi miyambo yanu, mwawapangitsa Mawu a Mulungu kukhala opanda mphamvu kwa inu.” Chabwino, ndicho chinthu chomwecho lero ndi Eva wauzimu, mwaona, mkwatibwi wauzimu wa lero, wotchedwa chomwecho, mpingo. Iye akuwatenga Mawu a Mulungu, ndipo iye sakuwalandira Iwo. Ndipo iye akulandira miyambo, mmalo mwake. Chotero, Mawu siali amphamvu kwa iye, mwaona, chifukwa iye akuyesetsa kubairamo kachikhulupiriro kake limodzi ndi Mawu, ndipo izo sizigwira ntchito. Tsopano, chimene ife tikuchisowa lero. . .

¹⁸⁵ Ine ndikungowerengabe ichi apa, *Herald of His Coming*, pa mitu yankhani, “Ife tikufuna mneneri kuti abwerere! Ife tikufuna mneneri kuti abwerere!” Ndipo ine ndikuganiza, pamene iye adzabwerera, iwo sadzadziwa kanthu za zimenezo. Basi. . . Ndiko kulondola. Izo nthawizonse zakhala ziri mwanjira imeneyo, mwaona. “Ife tikuchisowa icho,” chirichonse chimene inu mungachinene, “ife tikusowa mneneri kuti abwerere, yemwe ati adzabweretse Mawu a Ambuye, mopanda mantha. Ife tikukhulupirira kuti Baibulo linalonjeza zimenezo.”

¹⁸⁶ Tsopano, ine ndikudziwa M'bale—M'bale Moore ndi iwo, amadyera mnyumba yake, ndi china chirichonse, mkonziyo. Ndipo iye ndi munthu wabwino kwambiri amene—amene amayenda mu nsapato ya chikopa, ine ndikuganiza, mmodzi wa anthu abwino kwambiri. Koma, mukuona, iye akudziwa kuti ife tiyenera kukhala naye uyo. Ndipo Mlongo Moore, mmodzi wa akazi abwino kwambiri, wamng'ono. . . munthu wamng'ono wosauka, ndipo iwo amadzipereka.

¹⁸⁷ Ndipo iyo ndi imodzi mwamapepala abwino kwambiri pa ntchitoyi, mwa kulingalira kwanga, ndi *The Herald of His Coming*. Koma inu mukupeza kuti, iwo akupitiriza kufuula pa zimenezo, “Ife tikusowa mneneri! Ife tikusowa mneneri!” Mukuona? Mai! Ndicho chimene iwo amachikamba.

¹⁸⁸ Ndiyenyo apa ife tiri, lero, ndipo monga dzulo ndi lero, akulengeza pa wailesi, zimenezo. . . ndipo mipingo ya Baptisti ndi ina yotero, ikuti, “Ife sitienera kutengeka nawo Achikatolika, koma ife tizikhala ngati tikuyanjana nawo iwo.” Mukuona?

¹⁸⁹ Ndipo pomwe apa, Uthenga ukutulukira pomwe apa, kuti, “Khalani kutali ndi chinthu cha chiphe chimenecho!” Mukuona? Mukuona? “Angayende bwanji awiri limodzi pokhapokha iwo atagwirizana?” Kuwala ndi mdima sizingayanjane pamodzi. Pamene Kuwala kulowa mkati, mdima umatulukamo. Mukuona? Izo sizingakhoze. . . Champhamvu kwambiri! Inu simungazimitse Kuwala, ndi mdima. Koma inu mukhoza

kuwuchotsa mdima, ndi Kuwala. Ndiko kulondola. Ndipo Iye ndi Kuwala, ndipo Iye ndi Mawu. Mukuona? Tsopano, ndi zimenezotu pamenepo, kubwerera molunjika kumene. Inu simungawapangitse Iwo kunama kapena kuchita chirichonse cholakwika. Iwo amabwerera mmbuyo molunjika kumene kupita kumalowo kachiwiri. Inde, bwana.

¹⁹⁰ Monga ngati munthu wina akayamba, kuyesera kukangana ndi iwe; ngati iwe ukudziwa poti uyime, udziwe chimene iye amakhulupirira.

¹⁹¹ Basi ziri ngati kutenga kalulu ndi kumumasulira mu khola, ndipo iwe nkukhala utatseka una uliwonse. Ungoyima pa chipatapo; iye ayenera kubwereranso. Ndizo zonse ziripo kwa izo. Iwe unamumangirira iye mkati. Mukuona? Iye adzayenera kubwerera mmbuyo momwe waku chipatacho kachiwiri, chifukwa iyo ndi njira yokhayo yomwe iye angatulukirepo. Iye adzatulutsira mutu wake *pamenepo*, ndipo pafupifupi kuthyola khosi lake; ndi kumapita cha *apo*, cha *apo*. Udzangoyima ndi kumamuyang'ana iye, ndipo iye adzabwerera mmbuyo momwe. Mukuona? Ndizo zonse.

¹⁹² Ndiyo njira yokhayo yochitira. Kukhala ndi Mawu amenewo. Iwe ukhoza kumalengeza ponse pozungulira, ndi tizikhulupiriro tako, uzingothyola nazo khosi paliponsepo, koma uyenera kubwereranso ku Mawu awa. Mukuona? Inde, bwana. Ndi onse a Iwo.

¹⁹³ Tsopano, mwaona, iwo—iwo—iwo—iwo sakuwafuna Iwo. Iwo sakuwafuna Mawu a Mulungu. Chifukwa iye anagwiritsitsa ku miyambo yake, iye anawapangitsa Mawu a Mulungu kukhala opanda mphamvu.

¹⁹⁴ Chimodzimodzi tsopano, pa Eva wauzimu. Iye sakufuna . . . Iye akufuna kuti azisunga miyambo yake, ndi kuchoka ku Mawu a Mulungu. Iye akugwiritsitsa kachiwiri ku zipembedzo, ndi tizikhulupiriro tawo ndi miyambo ya akulu ake, mmalo motenga Mawu a Mulungu.

¹⁹⁵ Ndipo pamene lonjezo la Mawu, mmasiku otsiriza, lidzabweretsedwa kwa iye, iye sadzalilandira Ilo, chifukwa, ndi miyambo yake, monga mkwatibwi wa Chihebrani anachitira. Mawu enieni, ngakhale atawonetseredwa, kutsimikiziridwa, kuvomerezedwa, iye sadzakhala nawo Iwo. Chifukwa chiyani iye sadzatero? Chifukwa apo pali chomuyimira chake. Iye sangakhoze kuchita zimenezo. Ndiko kulondola. Iye sangapose chomuyimira chake. Mukuona? Ndipo izo zinanenedweratu kuti iye adzachita zimenezo, kotero inu muzemba bwanji chirichonse?

¹⁹⁶ Tsopano chinthu chokhacho choti muchite ndicho kungokhala wokondwa kuti inu muli mkati. Ndizo zonse. Mukhale mukuyembekezera zimenezo. Chabwino.

¹⁹⁷ Mulungu analonjeza, mmasiku otsiriza, kuti Iye adzawonetsera ndipo adzatsimikizira Mawu Ake kwa iye, ndipo komabe iye sadzachita zimenezo. Zonse zimenezo, Mulungu anamulonjeza iye, kudzera mwa antchito Ake, aneneri. Mulungu analonjeza, kudzera mwa Yesu Khristu. Mulungu analonjeza, kudzera mwa Yoweli. Mulungu analonjeza, kudzera mwa Paulo. Mulungu analonjeza, kudzera mwa Malaki. Yohane... Mulungu analonjeza, kudzera mwa Yohane mvumbulutsi, aneneri onse amenewo, ndendende basi chimene Uthenga wotsiriza ukanadzakhala kwa iye. Tsopano, ngati inu mukufuna kuwalemba iwo; ndithudi, inu nonse mukuwadziwa iwo: Yesu, Yohane 14:12; ndi Yoweli, Yoweli 2:38; Paulo, Timoteo Wachiwiri 3; Malaki, mutu wa 4; ndi Yohane mvumbulutsi, Chivumbulutso 10, seveni-tini, wani mpaka seveni-tini. Mwaona, ndendende chomwe chikanachitika tsopano! Ndipo, kwa mpingo, ndi chiyani Chimenecho? Mawu osandulika thupi atakhala pakati pa anthu Ake kachiwiri! Mukuona? Ndipo basi iwo osawakhulupirira konse Iwo.

¹⁹⁸ Inu mukudziwa zimene Yesu ananena pamene Iye anamuwona Iye...pamene Iye anachita zozizwitsa izo pamaso pawo, ndi kutsimikizira kuti Iye anali Mulungu? Anatsimikizira zimenezo, zomwe Iye anali kuchita. Iye anali. Iye anali atachita ndendende. Iye—Iye anati kwa iwo, Iye anati, “Oh, iwe, Kaperna, amene wadzikweza mpaka kumwamba ngati zintchito zikanakhala...ntchito zazikulu zikanakhala zitachitidwa mu Sodomu, zimene zachitidwa mwa iwe, iye bwenzi akuyimabe mpaka lero.” Ndiko kulondola. Ndipo mu Kaperna, Iye sanachitemo kalikonse koma kuchiritisa anthu pang’ono, ndipo anawauza iwo zinsinsi za mmitima yawo, ndipo anatulukamo. Uh-huh. Ndizo zonse. Mukuona?

¹⁹⁹ Iwo samadziwa zomwe ntchito zazikulu ziri. Iwo amaganiza kuti ilo limayenera kukhala dongosolo lopambana lalikulu kumene aliyense amaimirira, ndipo woweruza nkudzayankhulapo, ndipo—ndipo mabandi nkumaimba, ndipo zokongoletsa zikuwuluka, ndipo—ndipo akazi ovekedwa bwino, ndi zawo...ndipo akuyembekezera, ndipo onse ama Ph.D, LL.D, ndi zisoti zazikulu, zazitali, ndi makolala atatembenuzidwa, ndi chirichonse, iwo onse amayenera kulowamo. “Ndicho chinachake chopambana.”

Mulungu amati, “Ndizo zopusa.”

²⁰⁰ Ndipo Iye amabweretsa kenakake kakang’ono kamene sikamadziwa kusiyana kwa pakati pa mwina ma ABC, nkomwe, ndi kudzachita chinachake chimene chimangowuyika Mpingo weniweni pamoto. Ndipo ena onse a iwo amati, “Gulu la oyera-odzigudubuza.” Mulungu amachitcha *Icho* “chopambana,” ndipo dziko limachitcha *Icho* “chopusa.” Dziko limachitcha *icho* “chopambana,” ndipo Mulungu amachitcha *icho* “chopusa.” Mwaona, mosemphanitsa basi. Mukuona? Ndipo chinthu

chimene Mulungu walonjeza, Mulungu adzachichita ndipo wachichita. Mukuona? Ndi ife pano.

²⁰¹ Tsopano, komabe, iye akadali monga iye anachitira, Eva wa Chihebri. Iye sakanachita basi zimenezo. Inu mukanakhoza kuwukitsa akufa; inu mukanakhoza kuwona Mzimu wa Mulungu. Yesu anadzabwera, anadzitsimikizira Iyemwini kuti anali Mwana wa Mulungu. Poyamba, Iye anayamba kulalikira. Chabwino, iwo ankaganiza, “Chabwino, kukhala ngati Munthu-wachirendo. Ndi ndani Iyeyu, mulimonse?” Chabwino, chinthu choyamba inu mukudziwa, anthu anayamba kumati. . .

²⁰² Ndithudi, iwo anali atanena, mmbuyomo, pamene wotsogolera kubwera Wake anabwera, Yohane, iwo anati, “Kodi ndiwe Mesiya?”

²⁰³ Iye anati, “Ayi. Koma Iye waimirira pakati panu penapake.” Uh-huh. Mukuona? Bwanji? Iye ankadziwa, pamene uthenga wake unkachitika, chimene iye anali woti adzachite. Iye ankadziwa chimene iye akanati adzachite.

²⁰⁴ Chimodzimidzi monga Nowa anakhala akumuyang’ana Enoki. Pamene Enoki anapita, Nowa anati, “Kulibwino ndiyandikire ku chombo. Nthawi ili pafupi.” Nowa anapitirira kumamuyang’anitsitsa Enoki. Mukuona?

²⁰⁵ Ndipo Yohane ankayang’anira chizindikiro chimene Yesu anamuuza iye, kapena chimene Mulungu anamuuza iye, kuti aziyang’anapo. Iye anati, “Iye wayima pomwe pano tsopano, penapake pakati panu. Ine sindikumudziwa Iye, koma ine ndimudziwa Iye.”

²⁰⁶ Ataima pamenepo, iwo anati, “Kodi sindiwe Mesiya?” Anati, “Ife tatumidwa kuchokera ku likulu.” Uh-huh. Anati, “Akuluakulu, ndi onsewo, atituma ife kuno. Ngati iwe uli Mesiya, bwanji iwe sukubwera ndi kudzadziziwitsa wekha kumtunda uko, osati kumusi kuno mu gulu ili la zinthu kumusi kuno! Ubwere kumtunda uko ndipo ukadzizindikiritse wekha.”

²⁰⁷ Iye anati, “Ine sindine Mesiya.” Iye anati, “Ndine liwu la mmodzi wofuula mchipululu.”

²⁰⁸ Chimenecho chinapita patali pamwamba pa mitu yawo momwe icho chikanakhoza kupitira. Iwo sanadziwe kanthu za icho, mwaona, ndipo komabe iwo onse anali akumuyembekezera iye kuti abwera. “Koma sakanakhoza kukhala munthu ngati ameneyo. Oh, mai, icho chikanakhala chowopsya!”

“Ndiwe wochokera ku sukulu iti?”

“Palibe.”

“Kodi uli nalo khadi lako la chiyanjano?”

“Ndi chiyani chimenecho?” Mukuona?

²⁰⁹ Iye anali wodzozedwa wa Mulungu. Iye anati, “Pali chinthu chimodzi chimene ine ndiri nacho. Nkhwangwa yaikidwa

ku muzu wa mtengo.” Tsopano, ndizo zonse zomwe iye—ndizo zonse zimene iye anali nazo. Iye ankayankhula mu mayankhulidwe a munthu wa kuthengo, osati mmayankhulidwe a munthu wachipembedzo; njoka, ndi nkhwangwa, ndi mitengo, ndi zina zotero. Iye—iye sankayankhula mwa mayankhulidwe achipembedzo.

²¹⁰ Koma Yesu anati sipanakhalepo mneneri wonga iye. “Sipanakhalepo mwamuna wobadwa mwa mkazi, wonga iye, kufikira tsiku lake.” Uko nkulondola. “Iye anali woposa mneneri.” Iye anali mtumiki wa Pangano, anayima pakati pomwe pa—pa nyengo ziwiri, zikubwera mmenemo. Mukuona? “Woposa mneneri.”

²¹¹ Ndipo kotero ndiye—ndiye iwo sanamudziwe iye. Iwo sanamumvetsetse iye. Iye anali ngati munthu wa mtundu wokhala ngati wosamvetsetseka, kotero iwo sanamusamale iye, mwaona.

²¹² Kenako pamene Yesu anadzabwera, ndiye, ndipo ndithudi sanali oti amulandira Iye, Mnyamata wa akalipentala uyu, kunalibeko chinthu chonga chimenecho, ali ndi dzina lakuda pansana Pake, la “wapathengo.” Ndipo, Iye, iwo sakanapita kukawona Munthu ngati ameneyo.

²¹³ Koma, koma penyani chimene Mulungu anachita. Iye anatenga osaphunzira, osawuka, asodzi, anthu akuthengo, alimi, ndi mahule, ndipo anawasiya olemekizekawo atakhala pamenepo. Bwanji? Chiyani? Chifukwa chiyani Iye anachita zimenezo? Chifukwa chiyani Iye anachita chinthu choterocho? Kodi inu mungalingalire? Chifukwa chakuti anthu amenewo anamuzindikira Iye kuti anali Mawu. Tsopano tiyeni tingowayang’ana iwo miniti yokha.

²¹⁴ Apa pali nsodzi wosaphunzira wachikulire, wosakwanitsa kulemba dzina lake. Baibulo linati iye anali “mbuli ndi wosaphunzira.” Iye akubweretsa nsomba zake ndi kudzaziyika izo pansi. Akutsikira kumusi uko ndi kukawona chimene chikuchititsa phokoso lonseli. Koma pansi mkati mwa iye, iye ankadziwa kuti Baibulo linanena kuti Mesiya... Ahebri onse ankayembekezera Mesiya, chifukwa pankayenera kukhala chinthu Chamalemba chikuchitika pamene Iye abwera.

²¹⁵ Panali patabwera a mesiya ambiri, atawuka ndi kumati, “Ine ndine Iye,” ndipo anawatsogolera iwo kutchire, mwa mahandiredi, ndipo—ndipo anawonongeka ndi chirichonse. Koma, mwaona, izo zinali zakuti zimusokoneze Mmodzi weniweniyo pamene Iye akanati adzabwere.

²¹⁶ Ife takhala nazo zofunda za Eliya ndi zikhotho, ndi chinthu china chirichonse, koma izo—izo—izo—izo zimangosokoneza chabe chinthu chenichenicho pamene icho chibwera. Mukuona? Ndiko kulondola. Mitundu yonse ya anthu amene avala mikanjo ndi zovala, ndipo akwiridwa mu zophimba za mitundu yonse

ya zotembenuzidwa, ndi china chirichonse. Izo sizimati. . . Izo—izo zimangotsimikizira. Monga dola yabodza, imasonyeza kuti pali imodzi yabwino penapake, ngati iwe utangoyipeza iyo. Mukuona?

217 Kotero apa Iye akubwera. Tsopano olemkezeke awa anatulukira, ndipo iwo anali atakhazikika pa cholowa mmalo chawo kwambiri! “Bwanji,” iwo anati, “tsopano, ngati Mesiya abwera, Iye ndithudi adzabwera kwa Kayafa. Iye adzabwera ku chipembedzo chathu. Iye adzabwera kwa Afarisi.” Asaduki, “Ndizo zomwe inu mukuganiza! Iye adzabwera kwa Asaduki.” Ndipo apo iwo anali, mwaona, chinthu chomwecho chimene iwo ali nacho lero, tsopano.

218 Koma pamene Iye anabwera, icho chinali chachilendo. Iye adzabwera, oh, mosiyana kwambiri ndi zomwe iwo ankaganiza, koma Iye anabwera molingana ndi Mawu. Ndipo iwo sankawadziwa Mawu.

219 Ndiroleni ine ndinene chimenecho, kwenikweni, kotero kuti inu mu. . . icho chilowerere mpaka pansi. Ine ndikufuna ichi chimvetsedwe. Ndiro liri vuto ndi inu lero, mwaona, inu simukuwadziwa Mawu! Mukuona?

220 Yesu anati, “Inu mumakhoza kuzindikira mawonekedwe a mlengalenga, koma zizindikiro za nthawi inu simukukhoza kuzizindikira.”

Anati, “Ife tiri naye Mose.”

221 Kotero, anati, “Ngati inu mukanamudziwa Mose, inu mukanandidziwa Ine.” Sankamudziwa Mose, ndipo chotero iwo sankadziwa. Iwo ankangodziwa kachikhulupiriro kamene iwo anali atakapanga.

222 Tsopano tiyeni timutenge nsodzi wachikulire uyu. Akuyika dengi lake pansi. Anakankhira ndevu zake zaimvi pansi, ndi kumayenda chotsika, “Ine ndikukhulupirira ndikawona Yemwe uyo ali.”

223 M'bale anati, “Tiye. Tiye tipite kumusi kuno.” Anati, “Ndi Munthu yemwe uja. Ndi Munthu uja amene ankamunena tsiku lina. . . Ine ndinakhala ndi Iye usiku wonse wathawu. Iwe ukumudziwa Yohane, yemwe ine ndinali kukuuza za iye?”

224 “Eya, munthu wakuthengo uja kumusi uko! Eya, ine ndinamva za iye.” “Chabwino,” Simoni wachikulire, inu mukudziwa, anati, “Ine ndinamva za iye kumusi uko. Eya, wakhala ali kumusi uko, miyezi iwiri kapena itatu yapitayo, kumusi uko. Inde.”

225 “Chabwino, iye anati. . . Ndipo tsiku lina iye anali kuyima kumeneko, iye ananena chinthu chosamvetseseke. Iye anati, ‘Inu mukudziwa, apa Iye akubwera pakali pano!’ Iwo anati, ‘Iwe ukudziwa bwanji?’ Anayang’ana cha pamenepo; Munthu wamba chabe ataimirira pamenepo. Iye anati, ‘Ine ndikuwona Mzimu wa

Mulungu, ngati nkunda, ukutsikira pansi. Ine ndikumva Liwu likuti, “Uyu ndi Iye. Uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa mwa Yemwe Ine ndikukondwera kukhalamo.” Kenako iye anayenda mpaka mmadzi momwemo ndipo anamubatiza Iye, ndi zina zotero. Chabwino, pamenepo, iye anati iye anamudziwa Iye.”

226 “Oh, ine sindikudziwa,” Simoni anatero. “Ine ndazimva zonse za zimenezo, nthawi zambiri.” Koma apa iye akubwera. Koma pansi mu mtima mwake munali mbewu yokonzedweratu. Mukuona? Yesu ananena chomwecho. Kulondola. Akuyenda mpaka kwa Iye. Akuyenda kupita. Anati, “Ine ndipita ku msonkhano kumeneko ndikawone.” Akuyenda kukafika kumeneko.

227 Yesu anali atayima pamenepo, Munthu wamba wamng’ono chabe. Anayendera kumeneko. Iye anati, “Bwanji, dzina lako ndiwe Simoni. Ndipo dzina la abambo ako linali Yonasi.” Izo zinamuphwetsa iye. Chifukwa chiyani? Kambewu kakang’ono ako, ka Moyo Wamuyaya kanakhudzidwa mkati mmenemo. Inde, bwana.

228 Anati, “Dikirani miniti! Zakhala bwanji zimenezo? Inu simunandiwonepo ine. Ngakhalenso abambo anga Inu simumawadziwa, chifukwa iwo anali atafa kwa zaka. Koma apa Inu mwabwera, mukudzandiwuza ine zimenezo? Tsopano, ine ndikudziwa kuti Baibulo limati...” Tsopano, kumeneko si kubwerera ku zimene akuluwo amanena. “Koma Baibulo linanena kuti Mesiya akanadzakhala Mneneri. Ndi Uyo pamenepo. Ndi Ameneyo.”

229 Tsiku lina Iye anadutsira ku Samariya, akupita mmusi kudutsa kumeneko ndi gulu la Ayuda. Iye anawasiya iwo. Ndipo mkazi wamng’ono, wa mbiri-yoyipa uyu anatulukira, mwinamwake dona wamng’ono wokongola, inu mukudziwa. Ndipo iye anali atasiyidwa pa msewu, ali mwana. Ndipo iye anali akupita kumeneko. Mwinamwake iye anali kuganiza za chinachake. Iye anayenda mpaka kukafika kumeneko ndipo anayika chidebecho pansi. Ndipo iye anayamba kuponyera chotungiracho pansi, inu mukudziwa, kumatunga madzi. Ndipo iye anamumva Mwamuna akuti, “Ndibweretsere Ine akumwa.” Iye anayang’ana pozungulira, ndipo apo panakhala Myuda wokhala ngati wa zaka zapakati.

230 Iye anati, “Kuti, kodi Inu sindinu Myuda? Inu simuyenera kuchita zimenezo. Si chamwambo wake kuti Inu muyankhule kwa ine. Ine ndine Msamariya.”

231 Iye anati, “Koma ngati iwe ukanadziwa Yemwe iwe ukuyankhula naye, iwe ukanabweretsa... iwe ukanandipempha Ine kuti ndikupatse akumwa.”

232 Anati, “Chidebe Chanu chiri kuti?” Mukuona? “Chingwe Chanu chiri kuti?”

“Chabwino,” Iye anati, “Madzi amene Ine ndimapereka ndi Moyo.”

²³³ “Chiyani?” Mukuona? “Bwanji,” iye anati, “bwanji, inu nonse mumafuna muzipembedza mu Yerusalemu. Ndipo makolo athu ankapembedza. . .”

²³⁴ “Oh,” Iye anati, “izo nzoona, koma,” anati, “ife Ayuda timadziwa chimene ife tikuchipembedza. Koma,” anati, “iwe ukudziwa, nthawi ikubwera pamene—pamene anthu sadzapembedza mu Yerusalemu kapena mu phiri ili.” Iye anati, “Iwo—iwo azidzampembedza Mulungu mu Mzimu, chifukwa Iye ndi Mzimu, Mzimu ndi Choonadi.” Chabwino, iye anayamba kuphunzira, inu mukudziwa.

Ndipo Iye anati, “Pita ukamutenge mwamuna wako ndipo ubwere naye kuno.”

Iye anati, “Mwamuna wanga? Ine ndiribe mwamuna aliyense.”

²³⁵ “Bwanji,” anati, “izo nzoona.” Anati, anati, “Iwe wakhala ukuyenda nawo asanu, ndipo uli naye wa chisanu ndi chimodzi tsopano.” Ndipo anati, “Iwe wakhapapo nawo asanu. Ndipo—ndipo, iwe, iwe ukudziwa. Iwe wanena zooni.”

²³⁶ Penyani! Chinali chiyani chimenecho? Kuwala uko kunakhudza mbewu imeneyo. Iyo inali itagona mmenemo, imene inayankhulidwa ndi Mulungu. Inde, bwana.

²³⁷ Mbewuyo inali pa dziko lapansi. Pamene Mulungu anasunthira madziwo kumbali, ndipo dzuwa nkudzaigunda iyo, iyo inatulukira. Uko nkulondola. Mukuona? Ndizo zonse zimene iyo inkasowa, linali dzuwa. Inkangosowa kuwala. Inde, bwana.

²³⁸ Ndiyenyo pamene Mzimu Woyera, mwa Iye, unadzachotsapo moyo wake wakale, ndi kudzawonetsera icho kwa iye, Kuwala kuja kunadzaikhudza iyo. Iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri.” Iye anati, “Tsopano, ife tikudziwa, ine ndikudziwa zimenezo, kuti pamene Mesiya adzabwera, ndicho chimene Iye ati adzakhale. Ndipo ife sitinakhale naye mneneri kwa zaka mahandiredi. Ife sitinakhalepo naye mneneri woona, kwa zaka mahandiredi.” Ndipo iye anati, “Inu mukundiiza ine bwanji za mwamuna wanga, ndipo mwandiiza ine amene ndakhala nawo, ndi zina zotero. Bwanji,” anati, “Ine sindikuzimvetsa izi.” Anati, “Pamene Mesiya adzabwera, chabwino, Iye adzachita zimenezo. Koma Ndinu Ndani?”

Iye anati, “Ine ndine Iye.”

Chinali chimenecho. Mukuona? Hule!

²³⁹ Ndipo ansembewo anayang’ana pozungulira ndipo anati. . . Chabwino, iwo ankeyenera kuti akayankhe kwa gulu lawo. Anati, “Musapusitsike naye munthu ameneyo. Iye ali—iye ali ndi mdierekezi. Ndizo zonse.” Tsopano, ndiko kusiyana

kwake. Ndicho chinthu chomwecho lero. Mukuona? Chinthu chomwecho lero, chikugunda ndendende basi. Eya. Inde, bwana.

²⁴⁰ Iye, iye anadziwa zimenezo, chifukwa Kuwalako kunayikhudza Iyo. Iwo a-... Asodzi amenewo, anthu akuthengo, alimi, okhometsa-misonkho, mahule, iwo anawona mwa Iye chimene Malemba ophweka anati Iye akanadzachita. Ndipo Afarisiwo sanakhoze kuwona, chifukwa cha miyambo yawo...?...Iwo sanakhoze kuwona, chifukwa cha miyambo yawo. Koma wachiwerewere, alimi, ndi iwo onse, iwo anachiwona Icho, onse amene anali okonzedweratu. Pamene kukayikira kunakungunukapo, mbewuyo inayamba kumera. Ndiko kulondola.

²⁴¹ Kodi iye anachita chiyani? Iye anati, “Chabwino, ndine wokondwa kuti ndakumana ndi Mesiya”? Oh, ayi, m’bale. Mu mzinda momwe iye anapita. Iye anayiwala za madzi aja. Iye anati, “Bwerani, mudzamuwone Munthu Yemwe wandiuza ine zinthu zimene ine ndazichita. Kodi ichi si chinthu kumene chimene Lemba limati Mesiya adzachichita? Kodi ichi si ndendende chimenecho?” Ndipo anthu amakhoza kuwona chinthu chomwe chomwecho.

²⁴² Monga Yesu Khristu ananenera, mu Yohane Woyera 14:12, kuti izo zikanadzachitika kachiwiri. Iye ananenanso izo mu Luka, pamene Iye anati, “Monga izo zinali mmasiku a Nowa.” Momwe Mulungu anadziwonetsera Yekha mwa Munthu, ndipo ananena yemwe anali kuseri kwa Iye; ndi chimene Sarah anachita, kuseka mu hema. Ndipo Malemba onse awa, a Malaki, ndi ena otero, ananeneratu mmasiku otsiriza. Ahebri 4 anati, pamene “Mawu” adzabwereranso. Malaki 4 anati Iwo akanadzabwereranso mwa munthu. Ahebri 4 anati, “Mawu a Mulungu amazindikira maganizo amene ali mu mtima.”

²⁴³ Ndipo iwo akhoza kuchiwona icho chikuchitidwa, ndipo nkuchokapo kwa icho pomwepo. Miyambo yawo imachibisa icho ndipo imachipanga icho kukhala chopanda mphamvu. Chabwino, ife tiri apa basi. Ndizo zonse. Uh-huh.

²⁴⁴ Inu mukudziwa, Iye akhoza kuchita chinthu chomwecho lero. Iye akhoza kubwera powonekera pomwe ndi kudzachita zinthu zomwezo zimene Iye anazichita nthawi imeneyo, monga Iye ananena kuti Iye akanadzazichita. Mukuona? Iye analonjeza kuti adzachita zimenezo. Iye analonjeza kudzachita izo. Ndipo ngati Iye angachite chinthu chomwecho, mtumiki wa Laodikaya akuyenera kuti achite zimenezo.

²⁴⁵ Ndiyenso ngati mpingo wa Laodikaya uziwona izo zikuchitidwa, iwo adzachita ndendende basi monga momwe mpingo wa Chihebri unachitira pachiyambi. Um-hum. Ziribe kanthu momwe Iwo angakhalire otsimikiziridwa mwabwino, oh, iwo adzachita zimenezo, mulimonse. Oh, mai!

²⁴⁶ Tsopano, Iwo amanena kuti akanadzatero. Ife tikanadzabwerera ku Mawu apachiyambi, ndi kudzawonetseredwa monga kunalonjezedwa, kudzabwezeretsa kachiwiri Chikhulupiro, Chikhulupiro chapachiyambi, kachiwiri. Ndipo ngati Iye anadzizindikiritsa Yekha kuti Iye anali kukhala pakati pa anthu Ake, pa kuchita zinthu izi; Iye mpaka kujambulitsa chithunzi Chake, mwasayansi kutsimikizira izo. Ndipo komabe iwo osakhulupirira zimenezo. Ndipo kutsimikiziridwa, kulola diso la kamera kumujambula Iye atayima pamenepo, Lawi la Moto lomwelo, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Ahebri 13:8, kuwonetsera kuti zimenezo—ndi mwasayansi, ndi mwanjira ina iliyonse, mwasayansi mmadera auzimu. Mwanjira iliyonse imene izo—izo zikanakhoza kutsimikiziridwa, izo zatsimikiziridwa.

²⁴⁷ Ndipo, inu mukudziwa, iwo mwinamwake akanadzachita chinthu chomwecho. Iwo mwinamwake akanadzangoyendapo nthawi yomweyo ndi kudzachita chinthu chomwecho monga iwo anachitira.

²⁴⁸ Oh, Mulungu tithandizeni ife! Oh! Ife tingoimira apa. Koma, Mulungu tithandizeni ife kuti tiwone tsopano, pemphero langa, pamene ife tikubwera tsopano. Chifukwa, ine sindikufuna kukusangani inu mochedwa kwambiri. Mulungu tithandizeni ife kuti tiwone. Ine ndikukhulupirira kuti mwinamwake, Mzimu uli pakati pathu, iwo ukhala pakali pano kuti Iye atithandize ife kuwulula, kutsegula Chisindikizo ichi.

²⁴⁹ Tiyeni tiwerenge. Pamene tikuwona chikhalidwe chimene mpingo ulimo, ife tikuwona pamene iwo wakhala uli, tawona chimene iwo anachita, tinawona pamene iwo un kayenera kubwera, tinawuwona iwo pamenepo, ndipo tinawona zomwe iwo ankayenera kuti achite. Iwo anachita basi zimenezo. Tsopano inu mukuona pamene ife tiri? Inu muchite kuweruzako. Ine sindingakhoze kuweruza. Ine ndangokhala basi ndi udindo wowabweretsa Mawu awa. Basi monga Iwo aperekedwera kwa ine, ine sindingakhoze kuwapereka Iwo. Mpaka Iwo ataperekedwa kwa ine, ine sindingakhoze kuwapereka Iwo; palibe wina aliyense angakhoze.

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachitatu, ine ndinamva chamoyo chachitatu chikuti, Bwera ndipo udzawone. Ndipo ndinapenya, ndipo taonani kavalo wakuda; ndipo iye amene anakhala pa iye anali nawo masikero awiri mdzanja lake.

Ndipo ine ndinamva liwu kuchokera pakati pa zamoyo zinai, likuti, Muyezo wa tirigu wogula ndi ndalama, ndi miyezo itatu ya barley yogula ndi ndalama; koma onetsetsa kuti usapweteke mafuta ndi. . . vinyo.

²⁵⁰ Tsopano, Mwanawankhosa ali nalo Bukhu mdzanja Lake, akumatula Zisindikizo. Iye wamatula choyamba, chachiwiri,

ndipo tsopano Iye akumatula chachitatu. Ndipo pamene Iye akuchimatula icho, Mwanawankhosa akuchimatula icho, Chisindikizo Chachitatu, Chamoyo chachitatu. . .

²⁵¹ Tsopano ndi angati amadziwa momwe Chamoyo chachitatu chinkawonekera? Chinkawoneka ngati munthu. Choyamba chinkawoneka ngati mkango; chinacho chinkawoneka ngati mwana wa ng'ombe, kapena ng'ombe; ndipo chachitatu chinkawoneka ngati munthu, anali munthu. Ndipo iye anachimva—Chamoyocho, chi—Chirombocho. Cholengedwa Chamoyo, chonga munthu, chinati kwa Yohane, “Bwera, udzawone chomwe Icho chiri, chinsinsi ichi chimene chabisika.” Monse kudutsa mu zaka za chiwombolo, chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi, Izo zakhala ziri zobisika pansi pa Chisindikizo ichi, zomwe ziti zichitike. Tsopano, “Bwera, uwone chimene Icho chiri.”

²⁵² Ndipo kotero Iye akuchitsegula Icho. Bingu likuphulika, ndipo Mwanawankhosa akutsegula Zisindikizo.

²⁵³ Tsopano, ndipo Yohane akuyenda kubwera pamenepo, kuti adzawone chimene Icho chikanati chikhale. Kodi iye anawona chiyani? Iye anawona kavalo wakuda. Ndipo womukwera wake anali nayo miyezo, kapena masikero, mdzanja lake. Tsopano, ndicho chinthu choyamba chimene iye anawona. Pamene Mwanawankhosa anachilengeza Icho, anamatula Chisindikizocho, zitatero Chamoyo chinacho. . . Mwaona, Zamoyo zimenezo zikumasinthana, pa kulengeza, “Bwera, udzawone.” Ndipo Yohane, pamene iye anali atayima, mwinamwake monga *chonchi*, iye akuyenda mpaka apa, pamene Mwanawankhosa anatsegula, ndipo anapita patsogolo. Kawirikawiri. . .

²⁵⁴ Bingu likugunda, monga ife tinawonera mu Chisindikizo Choyamba. Ndipo iye akuyang'ana kuti awone chimene chiti chichitike. Ndipo iye akuwona munthu akubwera, poyamba, pa kavalo woyera. Iye akumuyang'ana iye akukwera mpaka mmusi. Ndipo mpaka mmusi akudutsa, Yohane akumuwona iye mpaka kumapeto. Iye akumuwona iye akubwera mmusi, pa kavalo wake woyera, ali nawo uta mdzanja lake, ndipo—wokwerapoyo ali nawo, ndipo iye alibe mivi ndi iwo. Ndipo chinthu chotsatira chimene iye akuchiwona, iye akutenga korona, akupitirirabe kumakwera akudutsa.

²⁵⁵ Kenako ife tikupeza kuti, ndiye, Mwanawankhosa, apa iye akubwera kachiwiri, Iye akudzatsegula china. Ndipo akuyang'ana. Tsopano apa pakubwera ka—kavalo wofiira. Munthu uyu ali ndi lupanga mdzanja lake. Iye akukwerabe mpaka mmusi kudutsa mu Lemba, mwaona, ali ndi lupanga ili mdzanja lake, ndipo anali woti akaphe ndi kukachotsa mtendere pa dziko lapansi.

256 Tsopano Mwanawankhosa akutsegula Chisindikizo china. China mwa Zamoyozo, chonga munthu, chinati, “Bwera, udzawone.” Tsopano iye akuyenda kupita pamenepo, kukawona chimene ichi chiri. Ndipo pamene iye akutero, apo pakubwera wokwera pa kavalo wakuda.

257 Tsopano, usiku watha, ife tinapeza kuti wokwera yemweyo amene anakwera kavalo woyera anali mmodzi yemweyo pa wofiira ameneyo.

258 Ndipo Liwu linati, mkati mwa Zamoyozo, linayitana pamenepo, mukuona. Pamenepo, akubwera kuti adzawone chimene icho chinali: Iye anali mu Zamoyo izi. Ndipo iye anawona kavalo wakuda uyu.

Ndipo pamene . . . liwu lochokera mkati mwa zamoyo zinayi linayitana uko, Muyezo wa tirigu wogula ndi ndalama, ndi—ndi miyezo itatu ya barley yogula ndi ndalama; koma onetsetsa kuti usapweteke—mafuta ndi vinyo. (Mukuona?)

259 Wokwera uyu, tiyeni timukambirane iye. Ngati mungazindikire wokwera woyamba uja, amene iye anali. Ndipo ife tinapeza, usiku watha, Mwamalemba, kuti wokwera wachiwiri anali ndendende munthu yemweyo, kokha kuti iye anali pa kavalo wina. Chinachitika ndi chiyani? Iye anasintha utumiki wake. Mukuona? Kulondola. Ife tinapeza kuti iye anali wotsutsakhristu, ndipo iye anali atasintha malo ake.

260 Ife tinapeza kuti pamene iye, poyamba, anali chabe kavalo woyera, iye anadzakhala chiphunzitso. Tsopano, ife tatenga chirichonse cha izi mobwerera kumene m’Malemba. Mukuona?

261 Tsopano, penyani pamene ife tiri, usikuuno, m’badwo wa mpingo wina uwo tsopano. Mukuona? Ife tikubwera mpaka ku m’badwo wa mpingo wachitatu tsopano. Mukuona? Ndendende basi pa m’badwo wa mpingo wachitatu, ndi chimodzimodzi basi monga kavalo wachitatu. Mukuona?

262 Tsopano, m’badwo wa mpingo woyamba, unali chiyani iwo? Achinikolai anali ndi chiphunzitso, mwaona, woyamba wokhawo. Chabwino. Ndiye kenako, chinthu choyamba ife tikudziwera, chiphunzitso cha Chinikolai ichi, icho chinadzakhala chovomerezeka ndipo chinali cholondola, chinayamba kuchitika. Ndipo iwo anamuveka korona munthu uyu. Kenako, mzimu uwu, wotsutsakhristu, unadzakhala mu thupi la munthu. Mukuona? Ndipo ife tikupeza kuti, kenako, iye akudzakhala mdierikezi mu thupi, nayenso; chiwandacho chikuchokapo, ndipo mdierikeziyo akudzalowamo.

263 Ndipo basi monga momwe mpingo uwo uliri, wa mtundu umenewo, mpingo wotsutsakhristu, ukupambana, momwemonso Mkwatibwi wabwera motsatira ndi zinthu zosiyanasiyana: kudzera mu kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi kumasuntha chopitirirabe,

mwaona, basi monga chomwecho. Kokha kuti, iwo anatenga chitsitsimutso chawo poyamba, ndipo Mpingo ukutenga icho potsiriza. Zaka zawo zitatu zoyambirira...magawo atatu oyambirira a iwo amene anadutsa mu m'badwo wa mdima; kenako lachitatu, magawo atatu, Mpingo ukutuluka: kuchokera ku kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera mkati: *Mulungu Mthupi* akuwonetseredwa pakati pathu. Apa iye akubwera mmenemo, monga wotsutsakhristu, monga mneneri wabodza, kenako chirombo, kenako mu m'badwo wa mdima. Ndipo Mpingo ukutuluka kuchokera mu m'badwo wa mdima umenewo: kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera: *Mawu Mthupi la Wokhulupirira*. Ndipo iye akupita mmusi. Uh-huh. Mukuona zimenezo? Iye akupita pansi. Mpingo ukupita mmwamba. Mukuona? Izo ziri basi mwangwiro monga izo zingakhalire. Oh, ndi zokongola. Ine ndikungozikonda zimenezo.

²⁶⁴ Wokwera uyu ali yemweyo, koma gawo lina la utumiki wake.

²⁶⁵ Gawo loyamba, kavalo woyera, mwaona, iye anali mphunzitsi chabe, basi mphunzitsi wotsutsakhristu. Iye anali wotsutsa Mawu a Mulungu.

²⁶⁶ Ndipo tsopano kodi inu mungakhale bwanji wotsutsakhristu? Aliyense amene amakana kuti Mawu aliwonse a izi si owona, ndi kuti akhale akuphunzitsidwa mofanana basi, ali wotsutsakhristu, chifukwa iwo akukana—ma—ma—ma—Mawu. Ndipo Iye ndi Mawu.

²⁶⁷ Tsopano, gawo loyamba, kavalo woyera, iye anali mphunzitsi chabe, koma mzimu wotsutsakhristu mu chiphunzitso chake ndi mawonekedwe ake. Iwo unali wosalakwa. Iwo sukanakhoza kupweteka kanthu, unkawoneka ngati; unkangopitirirabe chomwecho. Umo ndi momwe Satana amalowera mkati. Oh, iye ndi mbalame yothyathyalika.

²⁶⁸ Iye anamuza Eva, anati, “Tsopano, iwe ukudziwa kuti ukufunafuna nzeru. Iwe sukudziwa chimene chiri chabwino ndi choyipa.” Anati, “Tsopano, ngati maso ako akanatseguka, iwe ukanadziwa chomwe chiri.” Ndipo anati, “Chipatsocho ndi chosangalatsa kwambiri. Ndi chabwino. Ndi—ndi chosangalatsa kuchiwona. Iwe uyenera kuchidya icho tsopano. Iwe sukudziwa ngati icho chiri, kapena ayi, sichoncho iwe?”

“Ayi, ine sindikutero. Koma Mulungu anati ndisachite chimenecho.”

“Koma, oh, chabwino, ine ndikudziwa, koma . . .”

“Mulungu anati Iye . . . ife tidzafa.”

²⁶⁹ Iye anati, “Ndithudi Iye sadzachita zimenezo.” Mwaona, mokoma basi momwe izo zingakhoze kukhalira. Taonani chimene icho chinachita.

²⁷⁰ Uyang'aneni mzimu wotsutsakhristu uwu ukuwuka pakati pa mpingo woyambirira, chiphunzitso cha Chinikolai. *Nikao*, "kugonjetsa" anthu wamba, kupanga munthu woyera. Oh, icho chiri basi chos-... "Chabwino, ife tikungofuna chiyanjano. Bwanji, inu mwamwazikana kunja kuno; palibe amene akudziwa kumene wina ali. Ine ndikuganiza kuti ife tonse tiyenera kukhala nalo bungwe ndi kukhala osinthika basi. Mwaona, ife tizipita, kukaziyika tokha palimodzi. Ife tiyenera kupanga loji kuchokera mu icho." Ndipo ndicho chimene icho chiri. Palibe chinthu choterocho chonga Mpingo wa Chikhristu wa Methodisti. Umenewo si Mpingo; imeneyo ndi loji. Baptisti, umenewo si Mpingo; ndi loji.

²⁷¹ Ulipo Mpingo umodzi wokha, ndipo ndiwo Thupi lachinsinsi la Yesu Khristu. Ndipo iwe umabadwira mwa Iwo, ndiko kulondola, mwa kukonzedweratu. Uko nkulondola. "Onse amene Atate anandipatsa Ine adzabwera. Palibe munthu angakhoze kubwera pokhapokha Atate atamuyitana iye. Ndipo onse amene Iye anandipatsa Ine, adzabwera kwa Ine." Kotero, izo, ndizimenezo. Iye basi. . .

²⁷² Mwanawankhosa akukhala pamenepo, akupanga—akupembedzera, kufikira wotsirizayo atalowa mkati. Belu laling'ono lidzalira, ndipo Iye adzatuluka ndi kukatenga cholowa Chake pamenepo, mwaona, ndizo zonse; adzawubweretsa Mpingo Wake Kwawo, omumvera Ake. Ndipo adzamuponyera mdani Wake mu Nyanja ya Moto, ndipo omumvera ake onse adzapita mmenemo limodzi ndi iye, ndipo ndi zimenezotu. Kenako ife tidzayenda kumka mu Zakachikwi.

²⁷³ Wokwera yemweyo, tsopano. Gawo loyamba ili, iye anali wosalakwa. Ndipo lachiwiri, tsopano, ngati inu munapita pamwamba pang'ono, kuposerapo apo pang'ono; gawo lachiwiri, Baibulo linati iye akanadzakhala "akanadzapatsidwa korona." Ndipo iwo anamuveka korona munthu, munthu wapamwamba. Mwaona, anamuveka iye korona! Ndipo, ndiye, Baibulo silinamutche iye papa. Baibulo linamutcha iye "mneneri wabodza." Bwanji? Eya. Ndithudi, iye ayenera kukhala mneneri wabodza, mwa mzimu wake wotsutsakhristu, umene unkaphunzitsa kutsutsakhristu motsutsa Mawu apachiyambi. Chifukwa, ngati iye ankaphunzitsa motsutsa Mawu apachiyambi, anali wotsutsakhristu. Iye anali. Ndipo Mawu ndi Mulungu, mwaona, Khristu. Chabwino. Tsopano, zitatha zimenezo, ife tinamupeza iye ndiye atavekedwa korona. Ndipo pamene iye anavekedwa korona, tsopano, iye ndi wosalakwa kwambiri ndi wopanda chodzithandizira. Iye ndi kamunthu kakang'ono chabe.

²⁷⁴ Komano mu Msonkhano wa Nicaea, iye anapangidwa icho, ndipo Konstantine anamupatsa iye chuma chonse. Ndiye kenako kodi iye anachita chiyani? Kenako iye, mwaona, Satana,

anamupatsa iye mpando wake wachifumu ndi ulamuliro. Baibulo linanena chomwecho, monga ife tadutsira mu zimenezo.

²⁷⁵ Tsopano, chinthu chotsatira ife tinapeza, kuti mdierekezi amalamulira ndale zonse zomwe zinayamba zakhalapo konse kapena ziti zidzakhalapo konse. Ife tinapeza izo mu Mateyu 4:11. Ndipo tsopano ife tikupeza, ndiye, kuti Satana anali nazo kale ndale.

²⁷⁶ Koma iye akuyesetsa kuti awutenge Mpingo, kotero iye akupita uko kuti akawunyenge Iwo. Iye anakamutenga munthu wake wapamwamba, akumugwiritsa ntchito iye mu bungwe, ndi kumuveka iye korona “vicar,” mwaona, khristu. Khristu anagwira ntchito mmalo mwa Mulungu. Mwaona, munthu uyu ndi vicar, mmalo mwa Mulungu. Mukuona? Zofanana basi, “mmalo mwa Mulungu,” chimene iye akuyenera kukhala, vicar panso pa Khristu.

²⁷⁷ Tsopano, tsopano, pamene iye anachita zimenezo, ndiye kodi iye anachita chiyani kenako? Iyeyo, Satana, anatenga mphamvu yake yandale, imene iye anali nayo kale, ndipo anatenganso mphamvu ya chipembedzo, imene anavekedwa nayo korona kale, ndipo anaziya izo pamodzi.

²⁷⁸ Ndiye kenako anamupangira iye korona wina waku gehena. Ndipo iwo amene anali atamwalira, ngati iwo akanadzalipira ndalama zokwanira, iye akanadzawatulutsa iwo. Mukuona? Kotero tsopano iye ali—iye ndi wolowa mmalo wa Kumwamba, wa purigatorio, monga iye akufuna kuzitchulira zimenezo. Mulibemo chinthu choterocho mu Baibulo, mwaona, koma iye ankayenera kupanga chinachake. Baibulo linati icho chinachokera ku phompho lopanda malire, ndipo chikubwereranso mwanjira yomweyo. Ndipo, pa dziko lapansi, wolamulira!

²⁷⁹ Tsopano kodi iye anapatsidwa chiyani kumeneko? Poyamba, iye anali ndi uta, koma anali alibe muvi uliwonse. Koma tsopano iye ali ndi lupanga lamphamvu mu dzanja lake. Iye akhoza kuchita chinachake tsopano. Ndiye iye akulumpha kuchoka pa kavalo wake woyera; kavalo woyera akumukwerabe mpaka ku mapeto. Tsopano iye akukwera chiyani? Kavalo wofiira, magari, kavalo-wofiira wa magari. Iye kwenikweni akumukwera ameneyo. Oh, ndithudi. Tsopano iye wapatsidwa mphamvu yayikulu ndi lupanga lalikulu, kuti aphe, ndiye iye akukwera kavalo wake wofiira wa magari.

²⁸⁰ Ife tikuwona, kuchokera mu Chisindikizo Chachiwiri, chimene chinamatulidwa usiku wathawu, iye anali atachotsa mtendere padziko lapansi ndipo anaphana wina ndi mzake. Ndipo mbiriyakale yake yomwe ya ofera, ya mpingo wa Roma Katolika, imawonetsa kuti iwo anawapha Achiprotetanti sikisite-eyiti milioni, kuchokera mu nthawi ya Hippo Woyera wa...pambuyo pa Augustine Woyera waku Hippo,

mpaka fifitini handiredi ndi eyite chinachake. “Sikisite-eyiti millioni.” Schmucker’s *Great Reform*, ngati inu mukufuna kuwerenga zimenezo, *Glorious Reform*, kani, mwaona. Tsopano, sikisite-eyiti millioni olembedwa pa mbiriyakale ya ofera chikhulupiro! Pamene mmodzi wa wotchedwa woyera wawo anapeza vumbulutso lakuti aliyense amene sankagwirizana nawo mpingo waku Roma ankayenera kufa ngati wampatuko, chimenecho chinawakhazika chabe iwo mozungulira pamenepo. Mnyamata, iye anapita kukakhetsa magari! Iye—iye analumpaha pa kavalo wake woye-... , kapena, pa kavalo wake wofiira, ndipo iye anapita kukakwera. Oh!

²⁸¹ Tsopano mphamvu yake yaikulu ikubwera. Iye anapangidwa kukhala vicar wa Kumwamba, ndipo ankapembedzedwa ngati Mulungu. Wolamulira wa dziko lapansi, polumikizitsa mpingo ndi boma pamodzi, zinamupanga iye kukhala wolamulira pa dziko lapansi; anamupatsa iye korona pa zimenezo. Iye ankakhoza kupempherera miyoyo kuchoka ku purigatoriyo. Iye ankakhozanso kupembe-... Iye anali basi munga ngati Mulungu, pa dziko lapansi, mmalo mwa Mulungu. Pamodzi, iye anali nayo mphamvu yaikulu yakupha aliyense amene sagwirizana ndi kulamula kwake. Ndani angayankhule chirichonse kwa iye? Mpingo sungakhoze kuyankhula kanthu; iye ndi mutu wa iwo. Boma silingayankhule kanthu; iye ndi mutu wa ilo. Kotero, iwo anafa mwa mamillioni. Mipingo yonse yaing’ono iyo, m’bale, inaswedwa, ndi kuphedwa ndi kukanthidwa, ndi kudiyetsedwa kwa mikango, ndi china chirichonse. Mukuona? “Chinjokacho,” Roma, “chinamupatsa iye mpando wake ndi ulamuliro.” Baibulo linanena chomwecho. Mukuona? Kotero iye anakwera wofanizidwa wake, kavalo wofiira kudutsa mu magari a anthu, mpaka iye anadzakhala kavalo wofiira.

²⁸² Tsopano Yohane akumuona iye ali pa kavalo wakuda. Iye anasintho, kukhala chinachakenso.

²⁸³ Tsopano ine ndiyenera kuti—kuti ndiyankhule ichi basi momwe chabwerera kwa ine. Ndiyeneno ndipo ngati icho chabwera kwa ine ndipo nkusafanana nawo Malemba ena onse, ndiye kuti Mulungu sanandipatse icho. Mwaona, Malemba ayenera kutero, ena aliwonse, iwo ali chabe chinthu chimodzi chachikulu—chinthu chachikulu munga chimenecho. Lemba liyenera kugwirizana ndi Lemba limzake. Ndipo chirichonse chotsutsana ndi Lemba... Ngati Mngelo wa Ambuye uja akanandiuza ine chirichonse chimene sichinali Mwamalemba, ine sindikanamukhulupirira Iye. Mukuona?

²⁸⁴ Ine ndinanena, uko mu Chicago tsiku lina, pamene iwo onse mahandiredi a atumiki amenewo... Kodi alipo aliyense anakhalapo pa msonkhano umenewo? Ndithudi. Msonkhano umenewo mu Chicago, ine ndinati, “Tsopano, inu nonse mumanena zakuti muli ndi... Inu mumaganiza kuti munali

kundipiringizira ine mkati apa, pa chinachake.” Pafupifupi monga mmene ziliri mchipinda chino tsopano. Ine ndinati, “Ndi chiyani chimenecho? Inu muli nazo izo monditsutsa ine.” Ine ndinati, “Mzimu Woyera unandiwonetsa ine, mausiku atatu apitawo, pamene mmodzi aliyense wa inu akanadzakhala. Ndipo ife sitikanadzakhala umo... Mufunsemi Carl apa ngati izo si zolondola.”

²⁸⁵ Ndipo panali Hank ndi onse a iwo, “Ndiko kulondola.” Inu nonse munali kumeneko kukamvetsera.

²⁸⁶ Ine ndinati, “Tsopano inu muli nacho choti munditsutse ine, pa Kuphunzitsa kwanga. Ndiro lomwe liri vuto. Tsopano ine ndikufuna mmodzi wa inu abwere apa, ndipo tengani Baibulo lanu ndi kudzayima pafupi ndi ine, ndipo mudzachitsutse Icho.” Ilo linali gulu la chete kwambiri limene inu munalimvapo. Ine ndinati, “Vuto ndi chiyani ndi inu?” Ine ndinati, “Ndiye, ngati inu mukudziwa kuti inu simungakhoze kuyima mowatsutsa Mawu, ndiye chokani kumbuyo kwanga. Inu Madokotala Auzimu ndi chirichonse, ndi kumayankhula momwe, kudzidziwitsa nokha ngati ‘Dokotala,’ ‘Dokotala,’ ‘Dokotala.’ Ndipo ndine...” (Oh, M'bale Wood ndi ine ndimati “osazitsata,” kapena, “osadziwa.”) “Ine ndiribe maphunziro, sindinapitepo ku seminare iliyonse kapena sukulu. Koma inu mutenge Baibulo lanu ndipo mubwere apa ndi kudzayima pambali panga, mudzatsutse mbewu ya serpenti, ubatizo mu Dzina la Yesu, kapena chirichonse cha zinthu zimenezo zimene ine ndimaziphunzitsa.” Palibe aliyense ananena liwu. Inu nonse mukudziwa zimenezo. Ilo linali gulu lachete kwambiri limene inu munaliwonapo konse.

²⁸⁷ Mwaona, iwo amangokuwa ngati ine sindikudziwa chiyani. Tsopano, tsopano apa izo ziri. Ine sindimakhulupirira mu kukangana ndi anthu, koma pamene zifika pamalo amene iwo akuyesetsa kukukokera iwe mu icho. Ndipo ine sindikanapitako, koma Mzimu Woyera unandiuza ine, unati, “Pita mpaka kumeneko. Ine ndikayima pambali pako.”

²⁸⁸ Ndinawauza iwo, masiku atatu kapena anayi isanafike nthawi imeneyo. Inu nonse munali kumeneko ndipo munawamva Bambo Carlson ndi iwo, ndi—ndi Tommy Hicks. Ndipo onse a iwo anakhala pamenepo. Ndipo ine ndinapita, masiku atatu zisanachitike, ndipo ine ndinati, “Inu mukayenera kukalepheretsa malo amenewo.”

²⁸⁹ Iwo unali usiku wa mkuntho. Ine ndinali ndikuchititsa msonkhano. Iye anati, “Pita, ukayime pa zenera lija, pa chitseko chaching’ono chachitatu chija kumeneko.” Ndipo ine ndinapita kumeneko ndipo ndinakayima mkati mmenemo. Ine ndinayang’ana panja monga choncho.

²⁹⁰ Iye anati, “Iwo atchera msampha pa iwe. Iwo akakupempha iwe kuti ukayankhule pa Ministerial Association of Greater

Chicago.” Anati, “Iwo akuyikira msampha iweyo, pa kuphuzitsa kwako kwa Mawu Anga.”

²⁹¹ Iye anati, “Tsopano, iwo akalepheretsa malo amenewo kumeneko. Iwo sakawatenga iwo. Ndipo iwo akapita ku malo, amene akakhale a bulawuni.” Anati, “Akawoneka motere.” Ine ndinayima, ndipo ndinadziwona ndekha nditakhala pa kona; ndinayang’ana mmbuyo uko ndipo ndinawona. Ine ndinawawona iwo onse kumeneko. Ine ndinawawona iwo onse azitumiki atakhala pamenepo, momwe iwo anakhalira. Ine ndinawayang’ana iwo ponsepo. Ndipo Iye anati. . .

²⁹² “Oh,” ine ndinaganiza, “Ine kulibwino ndisapite kumeneko ndiye, Ambuye, ngati iwo ati akachite zimenezo. Ine sindikufuna kuti ndikapweteke kumverera kwawo kapena kukachita chirichonse cholakwika.”

Iye anati, “Pita. Ine ndikayima pambali pako.” Iye anatero. Ndiko kulondola.

²⁹³ Tsopano, inu nonse, pali mboni pomwe pano, munali mutakhala apo pomwe ndipo mukudziwa kuti izo nzoona. Uko nkulondola. Chabwino, inu muli nawo matepi kuno, nanunso. Koma, ndi zimenezotu, mukuona.

²⁹⁴ Tsopano, tsopano apa pali chinsinsi cha izi. Ndipo tsopano, Icho, pamene Icho chinawululidwa kwa ine molawirira mmawa uno, kuwala kwa tsiku kusanati. Ndiye ndinapita mwamsanga ku Lemba ndipo ndinayamba kuyang’ana, kufufuza izo. Apo izo zinali. Zitatu za izo, kufikira pano, mwamtheradi zatero, zawululidwa mwauzimu. Eya. Tsopano apa pali chinsinsi cha kavalo wakuda, molingana ndi chimene chinawululidwa kwa ine.

²⁹⁵ Iye anayamba kumukwera iye mu nthawi ya mibadwo ya mdima. Ndicho chimene kavalo wakudayo ankayimira, mibadwo ya mdima, pakuti iyo inali nthawi ya pakati pa usiku kwa okhulupirira owona amene anatsalira. Yang’anani tsopano mu m’badwo wa mpingo umenewo, m’badwo wa mpingo wapakati uwo, m’badwo wa mpingo wa mdima. Penyani momwe Iye akuti, “Iwe wangotsala ndi mphamvu pang’ono.” Apo panali pakati pausiku kwa iwo, kwa wokhulupirira owona. Tsopano penyani. Mwazochitika chiyembekezo chonse chinali chitachotsedwa ku Mpingo woona, pakuti munthu uyu ankalamulira zonse mpingo ndi boma. Kodi iwo akanachita chiyani? Mwaona, Chikatolika chinali chitatenga malo, zonse mpingo ndi boma. Ndipo onse, amene sankagwirizana nacho Chikatolika, ankaphedwa. Ndi chifukwa chake iye anali pa kavalo wakuda. Ndipo penyani chinthu chakuda chimene iye anachita, mwaona, ndiye inu mukhoza kuwona. Ndipo inu basi. . . Ngati inu mukuidziwa mbiriyakale yanu, penyani zimenezo, ndiye inu mudza. . . Chabwino, inu simudzasowa ngakhale kuidziwa iyo, kuti—kuti mudziwe Ichi. Tsopano

penyani. Chiyembekezo chonse chinali chitapita. Ndiye kavalo wake wakuda.

Tsopano, iye anakwera pa kavalo wake woyera, wothyathyalika.

²⁹⁶ Kenako iye anapatsidwa mphamvu; iye anachotsa mtendere, anapha mamillioni. Ndicho chimene iye ankakachita pamene anali kukwerabe akudutsa. Ndipo iye akuchitabe zimenezo. Mukuona?

²⁹⁷ Tsopano, apa iye ali pa kavalo wake wakuda tsopano, akutulukira. M'badwo wa mdima, iyo inali nthawi imeneyo. Pafupifupi basi nthawi imene mpingo unali utatha kukhazikika, ndi kukhala mu mphamvu, iwo anapangitsa befu china chirichonse. Ndipo anapita kudutsa, pafupifupi, mahandiredi ndi mahandiredi ndi ma handiredi a zaka, ndi chimene owerenga aliyense amadziwa monga mibadwo ya mdima. Ndi angati amadziwa zimenezo? Ndithudi, mibadwo ya mdima. Ndi ameneyo kavalo wanu wakuda, akuyimira m'badwo wamdima umenewo. Tsopano, ziyembekezo zonse zitapita; popanda chiyembekezo nkomwe. Chirichonse chinkawoneka chakuda, kwa okhulupirira apang'onowo. Tsopano, ndi chifukwa chake iwo ukutchedwa, ukuyimiridwa, ndi kavalo wakuda.

²⁹⁸ “Miyezo yake, kapena masikero ake, mdzanja lake,” mukuona. Kuyitanira kumeneko, “Muyezo wa tirigu wogula ndi ndalama, ndi miyezo itatu ya barley yogula ndi ndalama.” Mukuona, makamaka, zimenezo ndi, tirigu ndi barley ndi zakudya zachirengedwe zofunikira pa moyo. Ndi zimene amapangira buledi ndi zakudya. Koma, mukuona, iye anali kulipiritsa zimenezo. Izo zikutanthauza, kuti, iye ankawalipiritsa omumvera ake mtundu wa chiyembekezo cha moyo umene iye anali kutumiza kwa iwo, pomapanga... Iye anayambira mu nthawi yomweyo, kumawapangitsa iwo kuti azilipira mapemphero, kuwalipiritsa pemphero. Iwo akuchitabe zimenezo; kupembedzera.

²⁹⁹ Chifukwa, kodi iye anali kuchita chiyani? Kutolera chuma cha mdziko lapansi. Sikero, akumayeza, “Muyezo wa tirigu wogula ndi ndalama; miyezo itatu ya barley yogula ndi ndalama.” Wokwera pa kavalo wakuda, mwaona, iye anali kupanga... kuwalanda omumvera ake ndalama zawo. Pamene, Baibulo limaneneratu kuti iye wagwirizira, pafupifupi, chuma cha mdziko lonse. Monga ife tinanenera usiku wathawu za Russia, ndi zonse zimenezo, iwo akungotenga ndalama zonse ndi kungowalanda anthu chirichonse chimene iwo ali nacho, chirichonse. Koteru, ndi zimenezotu.

³⁰⁰ Tsopano zindikirani. Inu mukuona kumene kutenga ndalama kwa kale kuja, mu mpingo, kukuchokera? Chokaniko kwa zinthu zimenezo; kuti mumange bungwe, chinachake

chachikulu, cha ma dolla milioni apa. Ndipo—ndipo kodi inu mukumuona amene ali mayi wa zimenezo?

³⁰¹ Zikomo Inu, Ambuye. Oh, mai! Ndine wokondwa kwambiri. Inde, bwana. Chabwino. Chakhala chiri chisomo Chake. Ndizo zonse. Chabwino. Chabwino.

³⁰² Iyo inali nthawi yapakati pausiku. Kodi inu mukumvetsa zimenezo tsopano? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndipo apa iye akulipiritsa mtundu wa moyo, ndiye barley wake ndi zakudya, zachirengedwe; sizinali zauzimu, tsopano. Uyo anali barley, mwaona, kotero, ndipo mkate wa barley ndi mkate wa tirigu. Iye anali kulipiritsa moyo wa mtundu umenewo umene iye anali kuwupereka kwa omumvera ake. Kulipiritsa pemphero la wansembe, kuti awapempherere anthu achoke mu purigatoriyo. Kumawalipiritsa! Tsopano ine ndikuzitenga izi kuchokera mu mbiriyakale. Kumawalipiritsa, ine ndikuganiza, ndi kupembedzera, ine ndikuganiza, zomwe . . . aliyense pano akudziwa chimene chiri . . . Kupembedzera, ine ndikuganiza ndi chinachake chimene iwe uyenera kuchichita, inu mukudziwa, kudzitunduza kwinakwake. Winawake ayenera kulipiritsa zimenezo. Kubweretsa chuma cha mdziko kwa iye, kwa iyemwini, kuchilowetsa mu mpingo kumene. Ndipo iye akukwerabe. Oh, ndithudi iye akutero. Inde, bwana. Akanakwerabe!

³⁰³ Zindikirani. Apa pali gawo labwino tsopano. Zindikirani.

. . . *uwonetsetse* kuti *iwe usapweteke* vinyo uyu ndi mafuta.

³⁰⁴ “Zochepa chabe za Izo zomwe zatsalira kumeneko, koma usati uzikhudze Izo!”

³⁰⁵ Tsopano, mafuta ndi . . . amaimira Mzimu, Mzimu Woyera. Ine ndikupatsani inu ndime pang’ono ngati mukufuna kutero. Pali Malemba awiri. Mu Levitiko, 8:12, pamene Aroni, iye asanalowe mkati, ankayenera kudzozedwa ndi mafuta, inu mukudziwa. Ndipo mu Zakariya 4:12, za mafuta akubwera, akutsanuliridwa kudzera mmipope, ndipo anati, “Uwu ndi Mzimu Wanga, Mafuta.” Chinthu china, ngati mukufuna kuwona Mateyu, 14 . . . 25, apo panali namwali wopusa, kapena 25:3, namwali wopusa analibe Mafuta, analibe Mzimu. Ndipo Mateyu 25:4, namwali wochenjera anali nawo Mafuta mu nyali yake, wodzazidwa-Mzimu. Mzimu! Mafuta amaimira Mzimu. Oh, ulemerero! Chabwino. Inu mukumvetsa zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chabwino. Tsopano, mafuta amaimira Mzimu.

³⁰⁶ Ndipo vinyo amaimira kukondoweza kwa vumbulutso. Oh, ine—ine ngati kuti ndithamange pa malo onsewo. Ndikudabwa ngati ine sindinawadzutse oyandikana nawo, pamene Ambuye anandiwonetsa ine zimenezo, mwaona, “kukondoweza kwa vumbulutso.” Mukuona?

307 Mafuta ndi vinyo, mu Baibulo, zimagwirizana pamodzi, nthawizonse. Ine ndinatenga bukhu lofotokozera mawu ndipo ndinafufuzamo. Ulipo mndandanda wa izo, monga choncho—monga *choncho*, pamene vinyo ndi mafuta zimayendera limodzi, nthawi zonse. Mukuona?

308 Pamene Choonadi cha Mawu olonjezedwa a Mulungu chawululidwa mowona kwa oyera Ake amene adzazidwa ndi Mafuta, iwo onse amakondowedwa. Vinyo ndi kukondoweza. Ulemelero! Ine ndikukumverera Iko pakali pano. Kukondowedwa ndi chisangalalo, kufuula! Mukuona? Ndipo, pamene Iko kutero, Iko kumakhala nako kuchita komweko pa iwo kumene—kumene vinyo amachita pa munthu wachibadwa. Chifukwa, pamene vumbulutso laperekedwa, la Choonadi cha Mulungu, ndipo wokhulupirira woona wadzazidwa ndi Mafuta, ndipo vumbulutso nkuwululidwa, kukondowezako kumakhala kwakukulu kwambiri mwakuti Iye amamupangitsa iye kuchita mwachilendo. Kulondola. Ulemelero! Mwaona, ndiro limene liri vuto ndi iwo tsopano. Ndiko kulondola, zimawapangitsa iwo kuchita mosayembekezeredwa.

309 Tsopano, ngati mukufuna Lemba la izi, ingoyambani kuweringa Machitidwe 2. Kodi iwo ali kuti? Iwo anali ndi lonjezo limene linali litaperekedwa kwa iwo. Pamene lonjezo lonse la Mzimu Woyera linatsanuliridwa pa iwo. Ndipo anali . . . Ilo linali litatsimikiziridwa Mwamalemba. Tsopano, inu mukuona, a . . .

310 Bwanji ngati iwo akanati . . . “Tsopano, dikirani, Iye anatiuza ife kuti tiyembekezere pamwamba pano kwa utumiki wathu.” Ndipo atatha masiku eyiti, iwo akanati, “Chabwino, ine ndikuuza inu, anyamata,” Marko anati kwa Mateyu, “Ine—ine ndikukhulupirira kuti ife tiri nawo kale Iwo, amzanga. Kodi inu simukuganiza chomwecho? Mukuona, ife tiri nawo kale Iwo. Pamene ife tikuyembekezera pa utumiki wathu tsopano, ife tikungoyenera kuti tizipita kunja, kumakalalikira. Iye anatiuza ife kuti tidzabwere pamwamba pano ndi kudzayembekezera, ndipo awa ndi masiku eyiti takhala tiri muno.”

“Chabwino, tiyeni tiyembekezere kwa tsiku lina.”

311 Masiku naini anafika. Kenako Marko anabwera pamenepo, kapena—kapena—kapena mwinamwake mmodzi wa ena onse, Yohane, anati, “Ine—ine—ine ndikukhulupirira kuti ife sitikuyenera kuyembekezera motalikanso. Ine ndikukhulupirira kuti ife tiri nawo kale Iwo. Si choncho inu?”

312 Ndiye ine ndikukhoza kumuwona Simoni, chifukwa iye anali nawo makiyi, inu mukudziwa. “Tsopano yembekezzerani miniti, anyamata! Lemba liri nacho chinachake choti linene pa izi. Iye sanatiuze ife basi kuti tidzadikirire kwa masiku angati. Iye anati, ‘Inu mukakhale kumeneko kufikira! Inu mukakhale kumeneko kufikira uneneri wa Yoweli utafika pokwaniritsidwa, kufikira uneneri wa Yesaya utatsimikiziridwa.’”

³¹³ “Pakuti ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena Ine ndidzayankhula kwa anthu awa. Ndipo uku ndiko kutsitsimutsa.” Uyu ndiye vinyo amene watsanuliridwa. Kodi vinyo ndi chiyani, mu Baibulo? Kutsitsimutsa. “Uko ndi kutsitsimutsa kumene kumachokera mu Kukhalapo kwa Ambuye.” Mukuona? Izo—izo ziyenera kukhala Mwamalemba tsopano. Mukuona?

³¹⁴ Kotero, inu mukuona, vinyo amaimira kukondoweza kwa vumbulutso. Ndipo pamene Mzimu Woyera unagwa, ndipo iwo nkuwona Moto wa Mulungu ukugwera pa iwo, mai, zimenezo zinayambitsa kuwakondoweza iwo. Ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, iwo anakondowedzedwa kwambiri mpaka anthu makamaka anaganiza kuti iwo anali ataledzera, koma iwo anakondowedzedwa ndi vumbulutso. Ndi la Mulungu... Ndi izi apa! Vumbulutso lotsimikiziridwa ndi Mulungu, litapangidwa kumveka bwino kwa iwo, iwo anakondwera nalo Ilo. Mulungu analonjeza zimenezo. Apa icho chinawululidwa kwa iwo, ndi kutsimikiziridwa kwa iwo. Amen! Apa panali munthu atayima pamenepo, akuti, “Ichi ndi Chijachi! Uwu ndi Iwo!” Ndipo pamenepo Iwo unali ulipo, zikutsimikiziridwa ndi chizindikiro chomwecho chimene ife tiri nacho lero. Apo pali—ndi kumeneko kukondoweza mwa vumbulutso. Mukuona? Ndipo, tsopano, iwo anali nawo Iwo kwenikweni pamenepo.

³¹⁵ Ndi chifukwa chake Petro anakhoza kufika kunja uko, ndi kudzati, “Bwanji, inu amuna aku Yudeya, ndi inu amene mumakhala mu Yerusalemu, mvetserani kwa ine. Inu nonse Madokotala Azauzimu, mvetserani kwa zomwe ine nditi ndikuuzeni inu, mwaona.”

³¹⁶ Oh, nzodabwitsa bwanji! Kuwululidwa! Kuwululidwa! Iwo anakondowezeza kwambiri pamene iwo anachiwona icho chikutsimikiziridwa. Icho nthawizonse chimatero basi. Icho nthawizonse chimatero.

³¹⁷ Pamene ine ndiwona kuti Mulungu analonjeza kudzachita chinthu chinachake mu tsiku lino, pamene Iye analonjeza kuti adzamatula Zisindikizo izi mu tsiku lotsiriza lino! Ndipo inu simukudziwa chisangalalo chake, ulemelero, pamene ine ndinamuwona Iye akuwulula izi, nditayima pamenepo ndi kumawona izo zikuchitika! Ndipo ndikudziwa kuti ndidzamutengera munthu aliyense, kokamutsutsa: Iye sananepo konse chinthu chimodzi kwa ife koma chimene chinachitika mwanjira imeneyo. Ndiyeno kuwona chisangalalo chimene chiri mu mtima mwanga, pamene ine ndikuwona lonjezo Lake la masiku otsiriza awa, monga Iye analonjezera kuti adzachita zimenezo. Ndipo apa ine ndikuziwona izo zikutsimikiziridwa ndi kupangidwa kulondola mwangwiro. Ndine basi... Inu mumandimva ine ndikuti, “Ine ndikumverera mwachipembedzo.” Ndiro lomwe limakhala vuto lake. Kukondoweza kumakhala moyipa kwambiri, ine—ine—ine

basi—basi ndimafika pafupi kuyamba kumachita mwachilendo, inu mukudziwa. Kukondoweza, kuchokera ku vumbulutso! Chabwino.

³¹⁸ Iwo anadzakhala okondowezeza kwambiri, chifukwa cha—vumbulutso, limene iwo analitsimikizira, chabwino, lonjezolo. Tsopano, oh, mai! Pamenepo panabuka chisangalalo cha kukondoweza, mpaka anthu anati, “Iwo aledzera ndi vinyo watsopano,” pamene Mulungu anawulula lonjezo Lake kwa iwo. Ndipo osati kokha kuti Iye anawulula ilo, koma Iye anatsimikizira ilo.

³¹⁹ Ndicho chimene nthawizonse ndakhala ndikunena. Munthu akhoza kunena chirichonse, eya, iye akhoza kungokhoza kunena chirichonse; koma pamene Mulungu abwera mozungulira ndi kudzachitsimikizira icho!

³²⁰ Tsopano, Baibulo linati, “Ngati patakhala mmodzi pakati panu, yemwe akudzinenera kuti ali wauzimu kapena mneneri, ngati iye anena zinthu izi ndipo izo nkusachitika, ndiye musadzapereke chidwi kwa iye. Musadzamuwope iye, nkomwe. Musadzamuwope munthu ameneyo. Koma ngati iye anena icho ndipo icho nkudzachitika; ameneyo ndi Ine, mukuona. Ine, Ine ndiri mu chimenecho. Izo zikutsimikizira kuti ndi Ine.”

³²¹ Ndipo, ndiye, mkazi wamng’ono uja wa Chisamariya. Pamene Lemba linanena kuti Mesiya uyu akanadzachita zinthu izi, ndipo apa Iye anayima ndipo anadzachita zimenezo ndendende basi zomwe Lemba linanena. Iye anati, “Ndi Uyo pamenepo. Bwerani, mudzamuwone Mwamuna! Kodi icho si ndendende chinthucho chomwe Lemba linati chikanadzachitika?” Mwaona, iye anakondowezeza nalo vumbulutso. Nkulondola uko? Iye anakondowezeza nalo vumbulutso, pamene ilo linatsimikiziridwa. Mukuona? Uko nkulondola. Iye anadziwa kuti apo panali. . .

³²² “Ife tikudziwa kuti Mesiya akubwera, Yemwe akutchedwa Khristu. Ndipo pamene Iye adzabwera, Iye adzachita zinthu izi.” Iye anaziwona izo.

Ndipo Iye anati, “Ine ndine Iye.”

³²³ Zitatero kukondowezeza kunayambika. Ndipo pamenepo iye anapita, akufuula, ndipo mpaka kudutsa mu mzindawo. Iye anasiya mtsuko wake wakale wa madzi, ndipo anapita kumusi uko, ndipo anati kwa anthuwo, “Bwerani, mudzamuwone!”

³²⁴ Tsopano, ngati inu mukanangodziwa miyambo ya Kummawa, icho chinali cholakwika kuti iye achite zimenezo. Inde, bwana. Mkazi wa mtundu umenewo, palibe aliyense akanakhoza kumvetsera kwa iye. Ayi, bwana. Mukuona, iye anali ndi chilemba, ndipo pamene iye. . . Ngati iye akanapita mpaka mu msewu monga choncho, ndi kumakachita monga chomwecho, anthu a mumsewu sakanalabadira za iye.

³²⁵ Koma, m'bale, iye anali ndi Mawu a Moyo pamenepo! Iye anali atakondowezeke. Inu mukanakhoza... Izo zinali ngati kuyesetsa kuzimitsa nyumba, ikuyaka moto, pa tsiku la mphepo. Oh, apo pali chinachake chikuyikupiza iyo! Iye anali—iye anali wokonzeka. Inde. Iwo sakanakhoza kuchizimitsa Ichu. Uwo unali Moto wa Mulungu ukuyaka. Inde, bwana. Iye anati, “Ngati inu simukukhulupirira kuti ziri choncho, inu mungobwera kuno kumene msonkhano ukuchitikira. Ine ndidzakuwonetsani inu chimenecho.” Eya. Ndi zimenezotu. Eya. Inde, bwana.

³²⁶ Ndipo kotero anthuwo anapita kumeneko. Ndipo Iye sanachitenso icho nthawi ina. Koma iwo anadziwa ngati chinachake chinali chitachitika kwa mkazi ameneyo. Iye anali atasinthidwa, kotero iwo anamukhulupirira Iye. Inde, bwana. Iwo anakhulupirira pa Iye.

³²⁷ Chifukwa, “Chikhulupiro chimadza pakumva, pakumva lonjezo la Mulungu, Mawu a Mulungu, ndi kuwawona Iwo akupangidwa kukhala enieni.” Chifukwa, Iwo ndi mbewu. Ndipo pamene Iyo yabzalidwa, Iyo idzatenga Moyo. Iyo idzabereka basi chimene Iyo ikuchiyankhula. Ngati iyo siyitero, ndiye iyo si Mbewu ya Mulungu. Kapena, wofetsayo sanadziwe momwe angaifetsere Iyo; Iye sanatumidwe ndi Mulungu, kuti adzafetse Mbewu. Iye akhoza kukhala akufetsa Izo pamwamba pa thanthwe kapena chinachake. Mukuona? Kotero inu—kotero inu mukuona, wofetsa akamafetsa Mbewu, Mulungu amazisamalira Izo, Izo zimagwera mmalo oyenera, mwaona. Oh, mai!

³²⁸ Ndiye Ichu chikunena chiyani kwa wokwera uyu mu wakuda? “Usapweteke vinyo Wanga ndi Mafuta Anga! Usazikhudze Izo, vinyo Wanga ndi Mafuta! Ine ndangotsala ndi apang’ono okha a Iwo pansi kumeneko, koma akadalipobe apang’ono okha kumeneko. Eya. Tsopano iwe ukhoza kumapitirira kudutsa ndi kumayeza mtundu wonse wa moyo umenewo umene iwe ukuwupereka; izo ziri kwa iwe. Iwe udzalipira pa zimenezo pansi kumeneko. Koma pamene iwe uti upeze vinyo uyo ndi Mafuta, iwe uzisiye Izo zokha!” Oh, mai! Ngati ungathe, ngati iwe...

³²⁹ Mwa kuyankhula kwina, monga chonchi, “Ngati ungazipeze zina mwa Nkhosa Zanga zapang’ono, zomwe zadzazidwa ndi Mafuta Anga ndi vinyo, mukuona, vinyo ndi Mafuta a Mawu angwiwo, wawona, ndipo iwe ukuti uwaphe iwo. Chifukwa, iwe, iwe ukuchita zimenezo. Ndizo zimene iwe ukuchita. Iwe usawakakamize iwo kumanena chirichonse chakuti ‘Tikuwoneni Maria,’ kapena kuchita chirichonse monga chomwecho, kapena zina za tizikhulupiriro tako. Iwe uchoitse manja ako pa iwo. Iwo akudziwa kumene iwo akupita, pakuti iwo adzozedwa ndi Mafuta Anga. Ndipo pokhala odzozedwa nawo Mafuta Anga, iwo ali naye vinyo wa chisangalalo, chifukwa iwo akuwadziwa Mawu Anga a lonjezo, ‘Ine ndidzawaukitsa iwo

kachiwiri.' Usakawapweteke Iwo! Usapite kumakayesetsa kuti ukawasokoneze iwo. Chifukwa, ingokhala kutali kwa Izo. Ayi." Zonse. . .

³³⁰ Iye amawatsimikizira Mawu Ake ndi kuwabweretsa Iwo mkati. Iwo ankadziwa. Iwo ankadziwa kuti iwo akanadzawuka kachiwiri. Oh, momwe ine ndimazikondera zimenezo! Psyii! Iwo adzawuka kachiwiri. Apa pakubwera kavalo wakuda, akukwera tsopano, mibadwo ya mdima.

³³¹ Apo panapita kavalo woyera; ife tinawona chimene iye anachita, mwangwiro. Apa pakubwera kavalo wofiira; ife tinawona ndendende zomwe iye anachita. Apa pakubwera kavalo wakuda. Inu mukuona, iye akumakhala wokwera yemweyo nthawi zonse, chimene iye akuchita, kumatsika kudutsa mmibadwo.

³³² Tsopano ife tikupeza kuti, iye ankayeza izo ndi kumalipiritsa zimenezo, ndendende: tirigu, zachibadwa, moyo wachibadwa. Ndizo zomwe ankakhalira nazo moyo.

³³³ Koma, kuphiphiritsa; Mzimu, Mafuta; ndi chisangalalo cha vinyo. "Moyo wauzimu umenewo, usapweteke Iwo. Uwusiye Iwo wokha!" Apo ayi, "Roma, iwe usawakhudze Iwo! Iwo ndi Anga! Iwo ndi a Ine!"

³³⁴ Tsopano ndiri ndi chinthu china apa chimene ine ndikufuna kuti inu muchidziwe. Zindikirani, icho sichinali chimodzi mwa Zamoyo zinayizo chimene chinati, "Usakhudze Mafuta ndi vinyo." Kodi inu munazindikira zimenezo? Zamoyo zinayizo zinakhala zikuyankhula, koma. . . Yang'anani, ndiroleni ine ndingowerenga kuchokera apa, pang'ono pokha, mwaona, tsopano.

. . . *muyezo*, ndalama, *wogula—wogula. . . tirigu wogula ndi ndalama*, *ndi miyezo itatu ya barley yogula ndi ndalama*; *ndipo uwonetsetse kuti usapweteke vinyo ndi. . . mafuta.*

³³⁵ Tsopano mvetserani apa.

Ndipo ine—ndipo ndinamva liwu lochokera mkati mwa zamoyo zinayi. . .

³³⁶ Chinali chiyani Icho? Mwanawankhosa! Ameni! Izo sizinali Zamoyo zinayizo. Mwanawankhosa ananena zimenezo. Chifukwa chiyani? Iye akukatenga Ake Omwe. Amene ali a Iye. Iye wawawombola iwo. Mukuona? Ameni! "Usakhudze Mafuta amenewo!" Ayi, bwana. Osati Zamoyo zinayizo, koma Mwanawankhosa anali Mmodziyo amene ananena zimenezo. Ndipo, oh, mai! Mwanawankhosa! Osati. . . Zamoyo zinayizo sizinalengeze izi. Mwanawankhosa ananena, Mwiniwake.

³³⁷ Pamene Zamoyo zinayizo zinati, "Bwera ndipo udzawone," ndipo iwo anapita, ndipo iwo anakawona icho monga chomwecho.

³³⁸ Ndipo Iye anati, “Muyeze wa tirigu wogula ndi ndalama, ndipo kwa muye- . . . ndi wochuluka chotero monga *chonchi*, ndi barley wochuluka chotero.” Koma kenako Mwanawankhosayo anafuula, pakati pawo pomwe, anati, “Koma usapweteke vinyo ndi Mafuta!” U-huh. Ndiko kulondola. Oh, mai! Mvetserani kwa izo, “Usapweteke Izo, mnyamata, kapena iwe udzalipira chifukwa chochita zimenezo tsiku lina.” Oh, mai!

Naini-sarte.

³³⁹ Chabwino, mwa kupambana kwa kumvetsa kwanga, ndi mwakupambana momwe ine ndikuzidziwira, ndipo ndi zonse zimene ine ndikuzikhulupirira mu mtima mwanga, ndiro tanthauzo lowona la Zisindikizo zitatu zimenezo. Ine ndikufuna kuthokoza Mulungu chifukwa cha zimenezo. Ndipo ine ndinena ichi, kuti, ndiro vumbulutso limene Iye anandipatsa ine. Iye anapereka ilo kwa ine, vumbulutso la Zimenezo. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ife tikukhala mmasiku otsiriza.

³⁴⁰ Mawa usiku ife tidzatenga wokwera pakavalo wotumbululuka uyo. Ndipo tsopano ine sindikudziwa. Ine sindikudziwa. Mulungu akudziwa kuti izo nzoona. Ine sindikudziwa chinthu chimodzi cha icho. Ayi.

³⁴¹ Ine ndinayang’ana pa phunziro langa lakale limene ine ndinali nalo zaka zapitazo. Ine ndinamuwona M’bale Graham Snelling kanthawi kapitako; iye mwina akhoza kukhala kuti wapita panja. Koma, ine ndikukumbukira pamene ine ndinkalalikira kuno, kale. Ine ndinayang’ana umo kuti ndiwone zomwe ine ndinayankhula zaka zapitazo. Tsiku lina ine ndinali kudutsa mu Bukhu la Chivumbulutso, ine ndinawatenga okwera pakavalo onse anayi pa nthawi imodzi.

³⁴² Ine ndinati, “Kavalo woyera, umenewo unali mpingo woyambirira, sindikukayika.” Ine ndinawerenga zimenezo kuchokera mu bukhu la Adventisti. Ndipo ndinawerenga chinachake mmenemo. Ine ndinati, “Umenewo unali mpingo woyambirira umene unapita patsogolo, ukugonjetsa.” Ndipo wotsatira anali kavalo wakuda, ine ndinati. . . Ine ndayiwala tsopano chimene ine ndinachitcha kavalo wakudayo. Ine ndinati. . .

³⁴³ Kapena, “Kavalo wofiira,” kani, ine ndinati, “kavalo ameneyo mwinamwake akutanthauza kuti—kuti vuto likubwera, ndipo iye akutanthauza kuti nk'hondo zambiri zidzabwera, kapena chinachake monga chimenecho.” Ine ndinati, “Mwinamwake kudzakhala nk'hondo zambiri.” Ine ndinati, “Ndicho chimene chikanadzakhala.” Ndipo kenako ine ndinati, “Ka—kavalo wotumbulu- . . .”

³⁴⁴ Kapena, “Ka—kavalo wakuda,” ine ndinati, “ameneyo—ameneyo akutanthauza kuti—kuti mwinamwake padzabwera nthawi yakuda pa dziko lapansi, pamene nyenyezi zonse zidza—zidzasiya kuwala; dzuwa lidzalowa, ndipo mwezi sudzapereka

kuwala kwake.” Ine ndinati, “Ndicho mwinamwake chimene chikutanthauza.”

³⁴⁵ Ine ndinati, “Kavalo wotumbululuka, ameneyo akutanthauza kuti matenda ambiri akubwera.” Tsopano, ine sindikudziwa chomwe icho chikutanthauza. Koma, ndicho, uko kunali kutanthauzira kwanga kwa zimenezo nthawi imeneyo, chifukwa ine ndinangozitenga izo mopambana mmene ine ndikanathera, nditayima apa pa guwa.

³⁴⁶ Koma, oh, ine ndinali pafupi kunena chinachake! Chabwino. Hum! Oh! Mudza—inũ mudzaziwona. Muzingopenyetsetsa, mwaona.

³⁴⁷ Tsopano, oh, kodi ife sitiri okondwa chifukwa cha ora ili lomwe ife tikukhalamo! Pamene tikuchiwona chinthu chonsechi chikulunjika mmwamba, ine ndikuganiza:

Mafuko akusweka, Israeli akuwuka,
Zizindikiro zimene aneneri ananenera;
Masiku a Amitundu atha, ndipo zowopsya
zacheluka;

“Bwererani, O omwazika, kwa inu eni.”

Tsiku la chiwombolo layandikira,
Mitima ya anthu ikulephera ndi mantha;
Dzazidwani ndi Mzimu, nyali zanu muzikonze
ziziwala,

Yang’anani mmwamba, chiwombolo chanu
chayandikira! (Oh, mai!)

Aneneri abodza akunama, Choonadi cha
Mulungu iwo akuchikana,

Kuti Yesu Kristu ali Mulungu wathu;

Kodi inu mukukhulupirira Zimenezo?

Koma ife tidzayenda pamene atumwi
anapondapo.

Pakuti tsiku la chiwombolo layandikira,
Mitima ya anthu ikulephera ndi mantha;
Dzazidwani nawo Mzimu, nyali zanu
muzikonze ziziwala,

Yang’anani mmwamba, chiwombolo chanu
chayandikira!

³⁴⁸ Kodi izo si zodabwitsa? Ine ndikuzikonda zimenezo. Chiwombolo chayandikira.

Ndipo kudzakhala Kuwala mu nthawi ya
kumadzulo,

Njira ya ku Ulemelero ndithudi inu
mudzayipeza;

Mu njira ya madzi, ndiyo Kuwala lero;
Kumizidwa mu Dzina lofunika la Yesu.

Ana ndi akulu, lapani ku machimo anu onse,

Mzimu Woyera ndithudi udzalowamo mkati;
 Kuwala kwa kumadzulo kwabwera,
 Ndi zoonza kuti Mulungu ndi Khristu ali
 mmodzi.

Iye ndi Mawu! Oh, mai! Zodabwitsa!

Posachedwa Mwanawankhosa adzatenga
 Mkwatibwi Wake kukakhala nthawizonse
 pa mbali Yake,
 Khamu lonse la Kumwamba lidzasonkhanako;
 Oh, adzakhala mawonekedwe aulemelo,
 oyera onse atavala zovala zopanda banga;
 Ndipo ndi Yesu iwo adzadya Kwamuyaya.

Oh, “Dzadyeni,” Ambuye ayitana, “Dzadyeni;”
 Oh, inu mukhoza kudzadya pa gome la Yesu
 nthawi zonse;

Iye amene anadyetsa khamu lonse, nasandutsa
 madzi vinyo,

Kwa anjala akuyitana, “Dzadyeni.”

Oh, “Dzadyeni,” Ambuye akuitana,
 “Dzadyeni;” (Kudyerera pa Mawu!)

Inu mukhoza kudzadya pa gome la Yesu
 nthawizonse;

Iye amene anadyetsa khamu lonse, nasandutsa
 madzi vinyo,

Kwa anjala akuyitana, “Dzadyeni.”

³⁴⁹ Oh, mai! Kodi inu muli ndi njala? “Odala ali iwo amene amva
 njala ndi ludzu la chirungamo.”

³⁵⁰ Kodi mukumukonda Iye? Kodi mukumukonda Iye? Kiyi
 ya *Ine Ndikumukonda Iye*, inu mukudziwa. Tiyeni tonse
 tingoyima tsopano, ndipo tikwezere mmwamba manja athu
 ndi kudzifotokoza tokha kwa Iye. “Ine ndikumukonda Iye, ine
 ndikumukonda Iye chifukwa Iye anayamba kundikonda ine.”
 Chabwino, tonse limodzi tsopano.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye
 Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
 Nandigulira chipulumutso changa
 Pa mtengo wa Kalvare.

³⁵¹ [M'bale akuyankhula mmalirime—Mkonzi]. Molemekeza
 kwenikweni basi. Iye tiri naye wotanthauzira apa, M'bale
 Higginbotham. Ine sindikudziwa ngati iye ali pano usikuuno,
 kapena ayi. Iye tikufuna, tipeze zomwe Iye wanena
 kwa ife. Ingodikirani miniti chabe. Apa, apa... [Mlongo
 akutanthauzira.]

³⁵² Ndithudi, Ambuye alemekezeke! Chikhulupiro changa
 chakwezedwera mmwamba mwa Mulungu. Inu, inu

mukumukonda Iye, usikuuno, ndi mtima wanu wonse? Oh, mtamandeni Iye, ndi kunena kuti, “Zikomo Inu, Ambuye Yesu!”

³⁵³ Momwe ife tikukupatsirani Inu matamando, ndi mitima yathu yonse, Ambuye! Ulemelero kwa Mulungu!

³⁵⁴ Zingomupatsani Iye matamando, inu nonse anthu. Mulungu akhale ndi inu! 

63-0320 Chisindikizo Chachitatu
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

CHIVUMBULUTSO CHA ZISINDIKIZO ZISANU NDI ZIWIRI
(The Revelation Of The Seven Seals)

Mauthenga khumi awa analalikidwa ndi M'bale William Marrion Branham pa Marichi 17 mpaka pa Marichi 24, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., ndipo *Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri* chinapitirira pa Marichi 25 ku Sherwood Motelo. Titapeza matepi apachiyambi omveka ndi otsirizika kwathunthu, Mauthenga awa abwerezedwanso molingana ndi dongosolo latsopano. Kuyesesa konse kwapangidwa pochotsa molondola Uthenga wolankhulidwa pa matepi a maginito kupita ku tsamba losindikizidwa, ndipo atsindikizidwa mkatimu mosachotsera mawu ena.

Maufulu onse mu bukhu ili ndi osungidwa. Bukhu ili silingagulitsidwe, kapena kusindikizidwanso, kumasuliridwa mu zilankhulo zina, kapena kugwiritsidwa ntchito popezera ndalama wopanda kufotokoza kwa chilolezo cholembedwa cha William Branham Evangelistic Association. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org